



Chikoka cha Gulu la Amayi

*Buku Lothandiza
Ophunzira a Yesu*



**Gulu la Chikoka cha Amayi
(Women Impact Network)**

*Buku Lothandiza Mayi
Yemwe ndi Wophungzira wa
Yesu*

Losindikizidwa ndi bungwe la Association for:
International Discipleship Advancement (**AIDA**)
mogwirizana *ndi bungwe la* **Educational Resources**

Dzina: _____

Malo: _____

Dziko: _____

Date _____

BUKU LOTHANDIZA MKAZI AMENE NDI WOPHUNZIRA WA YESU

Copy wright © Association for International
Discipleship Advancement (AIDA) New Delhi, India
2013

Bukuli ndi cholemba chothandizira Gulu la Chikoka cha Amayi Logwirira Ntchito Pamodzi (WIN) lomwe limalimbikitsa amayi kuyamba kapena kuyambanso kukhala odzipereka pa udindo wawo monga ophunzira a Khristu oona; kuwapanga kukhala okangalika powapatsa zipangizo monga m'mabuku ndi njira zoti afikire nazo amayi anzawo ndi chidziwitso champhamvu chochokera m'Malemba—kutsogolera anthu amene sakhulupirira Mulungu kupita kwa Khristu, ndi kuwaphunzitsa kukhala ophunzira a Ake odzipereka ku udindo wawo.

*Maina otsatirawa ndi a anthu ochokera ku bungwe la
ERVAIDA) amene alemba zimene zili m'buku
Lothandiza Ophunzira a Yesu pa Ntchito Yawo
Yopindula Miyoyoli:*

Mbusa Shanta Rawate
Mayi Rhoda Dragomir
Mayi Caroline Akbar
Mayi Sheba Baiju
Mayi Martha Sparks
Mbusa Stephen Liversedge
Mbusa Rolanda Bowman
Mbusa Paul Brawn
Mbusa Stephen Rawate

Zamkatimu

Ulemu ndi Zothokoza

1. Udindo wa Wophunzira wa Yesu.....	1
2. Makhalidwe a Wophunzira wa Yesu.....	7
3. Mariya wa ku Betaniya.....	15
4. Moyo wa Tsiku ndi Tsiku wa Wophunzira wa Yesu.....	21
5. Mwa Khristu.....	31
6. Wophunzira wa Yesu ndi Maubale Ake.....	35
7. Wophunzira wa Yesu ndi Ntchito Yopindula Miyoyo.....	43

- Chifukwa Chopindulira Miyoyo, 43
- Umboni Wanu Monga Munthu Panokha, 44
- Kufalitsa Uthenga Pogwiritsa Ntchito Mabuku, 45
- Njira ya ku Roma, 47
- Buku Lopanda Mawu, 48

8. Mkazi wa ku Samariya :

<i>Wopindula Miyoyo/Mboni ya Khristu.....</i>	<i>57</i>
9. Naomi ndi Rute:.....	63
10. Priskila: Wopanga Ena Kukhala Ophunzira a Yesu.....	69
11. Bungwe la WIN ndi Wopindula Miyoyo.....	75
12. Kutsogolera Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN	79
Zoonjera.....	84



Ulemu ndi Zothokoza

Theima “Mama” Brawn anamwalira pa August 13, 2009, napita kukakhala ndi Ambuye. Apa nkuti patangotsala mwezi umodzi kuti akwanitse zaka makumi asanu ndi anayi (90). Iwo anayamba kutumikira Ambuye ngati mbusa wa mipingo itatu ali pa msinkhu wa zaka 13, ndipo atamaliza maphunziro awo a ubusa mayiwa anatumikira monga m’missionale mu Kontinenti ya Africa kwa pafupifupi zaka 45, pamodzi ndi amuna awo a Dr Willys K. Brawn.

Mama Brawn ndi amene anakhazikitsa utumiki wa AIDA Women’s Conference m’dziko la India. Ngakhale anadwala kansa ya m’mpaha mu zaka zitatu za kumapeto kwa moyo wawo, iwo anapitirizabe kuyenda maulendo opita ku madera osiyanasiyana a m’maiko monga India, Napal, Bangladesh, ndi Myanmar kuphunzitsa ndi kupereka zipangizo kwa akazi ena mu mpingo, kuwakonzetsera ku ntchito yochitira umboni ndi kufalitsa uthenga wabwino. Kupezeka kwawo pa nsanja yolalikira Mawu a Mulungu kunali chilimbikitsa chopambana komanso uthenga wamphamvu kwa amayi anzawo amene amawalalikirawo.

Ndemanga zotsatirazi zikuonetsera mmene moyo wa Mamma Theima Brawn unakhudzira miyoyo ya amayi ena.

“Ine ndaphunzira kuti ngati Mamma Brawn angathe kutumikira Mulungu iwo atakalamba ndiye kuti nanenso ndikhoza kutumikira Ambuye nthawi ina iliyonse, kulikonse, mu zochitika zilizonse komanso ngakhale pa msinkhu wina uliwonse (Mbusa Jane Thomas Himachal Pradesh)

Ine ndaganiza kuti ngati Mamma Brawn angaoloke nyanja zisanu ndi ziwiri kupita ku madera kukatumikira Ambuye, nafenso tiyenera kupitiriza kutumikira mu mpingo (Roshani Phillips, Varanai, U. P.)

Kuona Mama Brawn atakhala tsonga kulankhula nafe tsiku lonse zinandilimbikitsa kupitiriza kufalitsa uthenga wabwino (Caroline Akbar, Nagpur, Maharashtra).

Awa ndi mawu amene Mama Brawn analankhula mu uthenga wawo womaliza:

“Ntchito yofalitsa uthenga wabwino sinathe ndipo ikudikira anthu oti aipitirize. Ntchito yaikulu kwambiri imene ife tili nayo pa dziko pano ndi yolalikira uthenga wa Ambuye wathu Yesu Khristu, ku Peru kapena ku West Bengal, kapena ku maiko ena komwe sikudafikebe uthenga wa Khristu. Kumbukirani kuti ntchitoyi sinathe. Mulungu akudalitsemi pamene mukukangalika kuyesetsa kufalitsa Nkhani Yabwinoyi.”

Ndithudi, ntchito yolalikira uthenga wabwino sinafike kumapeto! Wophunzira aliyense wa Yesu Khristu ayenera kukhala mboni Yake. Kutsogolera ena kwa Khristu ndilo khalidwe lofunikira kwambiri la wophunzira woona wa Yesu. Ndi pemphero lathu kuti khalidwe chilichonse cha Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN) chikhale chopindula miyoyo kupyolera mu mphamvu ya chisomo cha Mulungu, kuti chibale chipatso chochuluka kwa lye. (1 Yohane 15:1-2, 6).

1

Udindo wa Wophunzira wa Yesu

Vesi Lotsogolera: 1 Akorinto 9:19



*“Pakuti pokhala ndinali mfulu kwa onse,
ndinadzilowetsa ndekha ukapolo kwa onse,
kuti ndipindule ochuluka.”*

Udindo womaliza umene Yesu anapatsa ophunzira Ake unali woti”...**mukani phunzitsani anthu a mitundu yonse**..... (Mateyu 28:19). Liwu loti ophunzira limatanthauza aphunzi: anthu amene akuphunzitsidwa. Kunena zoonā, m’ma Baibulo angapo otanthauziridwa mosiyana, vesili limati **“Mukani...phunzitsani anthu a mitundu yonse . . .”** Vesi 20 likufotokoza momveka bwino kuti cholinga cha chiphunzitso chimenechi ndicho: “kuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani.” Ophunzira a Khristu si anthu amene amangophunzira kokha ziphunzitso Zake, koma iwo ndi anthu amene amati akaziphunzira amazisunga. Popeza ziphunzitso Zake zimaphatikizira Utumiki Waukulu, ophunzira oona a Yesu ndi amene amati akaphunzira, pamapeto pake nawonso amapanga ena kukhala ophunzira Ake ndi kuwaphunzitsa kusunga zonse zimene lye walamulira.

Mu utumiki wa Yesu padziko lapansi pano munali ambiri amene anamutsata. Makamu anali kumuzinga lye kuti awachize ku nthenda zawo (*Yohane 8:16*). Anthu miyandamiyanda anali kumutsata poona zozizwa zimene lye ankachita. (*Mateyu 6:2*). Ambiri a anthuwo ankati cholinga chawo chinali kukhala ophunzira Ake ndi kuphunzira kuchokera kwa lye. Koma pamapeto pake ambiri a iwo anamuthawa (*Yohane 6:66*). Komabe ophunzira Ake oona anali anthu amene anasiya zonse ndi kumutsata kufikira kumapeto a moyo Wake, komanso moyo wawo wa padziko lino lapansi (*Marko 10:28*). Iwo anali kumutsata ndi kumakhala naye monga bwenzi la pamtima, kuphunzira choonadi chakuya kuchokera kwa lye, ndi kusanduka “asodzi a anthu” mu utumiki Wake.

Malingana ndi buku lamatanthauzo a mawu la Chingezezi la American Tract Society, “Wophunzira wa Khristu watchulidwa monga munthu amene amakhulupirira chiphunzitso cha Yesu, amene wakhazikika pa nsembe Yake, amene walandira Mzimu wa Khristu ndipo ali mwa Iye, amene akutsanza chitsanzo Chake, ndi kumagwira ntchito Yake tsiku ndi tsiku.” Izi zikusonyeza kuti kukhala wophunzira wa Yesu ndi ndime imene imadza pambuyo pa kulandira chipulumutso; chipulumutso ndi chiyambi chabe cha kukhala wophunzira wa Yesu. Kuti munthu apulumutsidwe, iye ayenera kuyamba wakhulupirira kaye mwa Yesu. Chipulumutso chimadza “ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro.” **“Ndiipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu.”** (Aefeso 2:8). Koma dongosolo la kukhala wophunzira wa Yesu ndi chinthu chimene chimadza pambuyo pa chipulumutso, ndi cholinga choumba miyoyo yathu kukhala yotsanza chitsanzo cha Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu, ndi kuchita malamulo Ake, kumtumikira Iye, kukhala okhulupirika kwa Iye kufikira pamene imfa idzatitenge kupita nafe pamaso Pake.

Kuti wokhulupirira akhale wophunzira wa Yesu zimafunika kuti iye akhale wosunga mwambo ndi wodzipereka kwathunthu kwa Mbuye wakeyo. Udindo wa wophunzira wa Yesu ndi wokhudzana ndi kuphunzitsa komanso kuphunzira. Munthu amene akupanga wina kukhala wophunzira wa Yesu amayenera kumuphunzitsa munthuyo, ndipo munthu wopangidwa kukhala wophunzirayo akuyenera aphunzire kuchokera kwa mphunzitsi wakeyo. M'mabuku anayi a uthenga wabwino ife tikuonamo Yesu akuphunzitsa ophunzira Ake; m'buku la Machitidwe ife tikuwerengamo za momwe okhulupirira atsopano anapitirizira kuphunzira Mawu a Khristu modzipereka kuchokera ku ziphunzitso za atomwi. Ophunzira a Yesu anapanga anthu ena kukhalanso ophunzira Ake; ndipo onsewo anatchedwa Akhristu (*Machitidwe 11:26*). Chipangano Chatsopano chonse chinali (ndipo chikupitirizabe kukhala) Mawu a Mulungu opita kwa ophunzira Ake amene amatchedwa Akhristu. Chotero, tanthauzo la kukhala wophunzira wa Yesu ndilo kukhala molingana ndi chitsanzo cha Khristu, khalidwe lomwe lafotokozedwa m'Malembu.

Mosiyana ndi chipulumutso chimene ndi chochitidwa ndi Mulungu yekha, kukhala wophunzira wa Yesu kumachitika kupyolera mu mgwirizano wa pakati pa Mulungu ndi ife anthu. Pamene tapulumutsidwa ndi Mulungu, ife timadzazidwa ndi Mzimu Woyera, amene amatithandiza kukhala moyo wokondweretsa

Mulungu (*Yohane 14: 26; Machitidwe 5:32; 1 Akorinto 12:36*). Ngakhale zili zoonza kuti palibe chimene tingachite kuti tidzipulumutse tokha, ifetu timayenera kuchitapo kanthu pa nthawi yomwe Mzimu Woyera akutithandiza kukhala ophunzira a Yesu. Baibulo likuti Mzimu Woyera adzachita umboni za Yesu, ndi kupereka ulemmero kwa lye (*Yohane 15:26; Marko 16:13-14*). Sitingakhale ophunzira a Yesu abwino ngati ife sitili mu ubale komanso mgwirizano wamphamvu ndi Mzimu Woyera nthawi zonse, yemwe adzachitithandiza kukwaniritsa mfundo zonse zotiyenereza kukhala ophunzira a Yesu. Iye amachita izi pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu m'miyoyo yathu. (*Yohane 16:13-15*).

Ngati mukufuna kukhala wophunzira wa Yesu Khristu, inutu monga wophunzira Wake muyenera kumvera malangizo amene ali m'Mawu Ake, ndi kukhala wokonzeka kulandira thandizo la Mzimu Woyera, kuphunzira ndi kumvera malamulo onse amene mwalamulidwa kutsatira. Inutu ndi amene muyenera kusenza mtanda wanu, kudzikana nokha ndi kumutsata lye (*Marko 8:34*). Inu ndinu amene mumapereka thupi lanu mpatso yopatulika, yokondweretsa Mulungu, mutadziwa ndi kukumana ndi chisomo cha Mulungu (*Aroma 12:1*). Ndinu amene mumaleka kukonda dziko lapansi ndi zinthu za dzikolo (*1 Yohane 2:1*). Ndinu amene mumasankha kukhala wosunga mwambo ndi kudzikana kukhala molingana ndi makhalidwe, machitidwe, nzeru, kapena miyambo ya dziko lapansi, mmalo mwake inu mumakhala molingana ndi chifuniro changwirowo cha Mulungu (*Aroma 12:2*). Pamene mwakonzeka kudzipereka ndi kulola Mzimu Woyera kukuumbani m'khalidwe "longa la Khristu" amene anayamba kale kugwira ntchito yabwino ya chipulumutso mwa inu, ndipo adzaipitiriza ndi kuimaliza ndithu (*Afilipi 1*). **Ndipo chipatso cha Mzimu cha kutsatira Yesu kwanu sichidzangopanga** khalidwe longa la Khristu mwa inu kokha, koma khalidwe lotero lidzakhalanso mwa onse amene inu mudzawapange kukhala "asodzi a anthu." Khalidwe lanu monga wophunzira wa Yesu lidzapangitsa ena kukhalanso ophunzira a Yesu potsanza chitsanzo chanu, kubala zipatso popanga ena ambiri kukhala ophunzira oona a Yesu.

Umu ndi momwe uyenera kukhalira moyo wa Mkhristu aliyense. Ichi ndicho cholinga cha Khristu mu Utumiki Waukulu. Popeza chiwerengero cha Akhristu ndi chochepa kwambiri pakati pa anthu a chikhalidwe chathu, ifetu tili ndi ntchito yaikulu kwambiri yophunzitsa anthu ambiri- a mitundu yonse, ndi mafuko onse, ndi manenedwe onse, kupulumutsa otayika ku chionongeko chosatha

ndi kuwapanga iwo kukhala ophunzira a Khristu. Komabe ngakhale zinthu zili chomwechi, zochitika za dziko lathuli zimabweretsa mavuto otsatirawa:

(1) Chiwerengero cha anthu: “M’dziko la India muli magulu ambiri a anthu amene pakati pawo palibe Akhristu, mipingo, kapena atumiki koposa chigawo china chilichonse cha dziko lapansi. Dziko la India ndi lomwe lili ndi chiwerengero chachikulu cha anthu omwe sanafikiridwe ndi uthenga wa Chikhristu kuposa chigawo china chilichonse pa dziko lapansi (Operation World, 7th Edition, 2010, masamba 405-417). Ntchito yofalitsa uthenga wa Chikhristu m’dzikoli ndi yaikulu kwambiri moti alaliki ndi abusa olembedwa ntchito sangaikwanitse paokha popeza chiwerengero chawo ndi chochepa kwambiri m’dzikoli.

(2) Mmene Akazi kapena Amuna Amaonedwera: M’dziko la India akazi adakakumanabe ndi zopinga zokhudza ufulu wawo kamba ka kuchuluka kwa zinthu zimene zikuopseza chitetezo ndi thanzi lawo, zimene zimachitidwa ndi anthu a m’nyumba mwawo komanso ngakhale a kunja. Ngakhale masiku

ano pamene chikhalidwe cha moyo chikusintha kwambiri, akazi ambiri m’dzikoli amadzimva kuti ndi anthu opanda mphamvu komanso chiyembekezo. Iwo amalira, kufunsa, ndi kudandaulira ku lamulo. Iwo amayesetsa kuti maufulu awo adziwike, kuti nawo atengedwe monga anthu ofunikira, ndi kutsimikiziridwa kuti nawonso ndi anthu. Koma kunena zoono, iwo sadziwa kuti chosowa chawo chachikulu ndi chazimu komanso chosatha. Kodi ndi ndani amene angawaonetsetse kuunika kwa lye amene anafa ndipo tsopano ali ndi moyo, kuti awapange iwo kukhala anthu ofunikira?

(3) Kusowa Chidziwitso: Masiku ano, Mulungu akugwira ntchito mwamphamvu kwambiri, ndipo anthu ambiri akudza kwa Khristu. Pakati pa okhulupirira atsopanowa pali chiwerengero chochuluka cha akazi amene akusoweka kuphunzitsidwa za mmene angakhalire ophunzira a Yesu. Kafukufuku waonetsa kuti ngakhale amayi amenewa akukula m’chikhulupiriro ndi mu ubwino wa Mulungu, iwotu

akufunika kuphunzitsidwa Mawu a Mulungu. Pa chifukwachi, ambiri a iwo akakumana ndi zovuta komanso chizunzo chocho-kera kwa adani awo, iwo amasiya chikhulupiriro chawo. Ku mbali inayo, ngati iwo ataphunzitsidwa kukhala ophunzira a Yesu oona, iwotu adzakhoza kulimbikitsidwa kutumikira mu ntchito yofalitsa uthenga wa ufumu wa Mulungu nadzakhala okonzeka ndi olimbika monga khamu la njuchi, kubweretsa ena kwa Khristu.

Chotero, ife tikusowa atumiki ambiri a Mulungu, mboni zambiri za Khristu komanso anthu ambiri opanga anthu ena kukhala ophunzira a Yesu pakati pa amayi. Atsogoleri angapo a mpingo azindikira ndipo afotokozapo zoti amayi amagwira bwino ntchito yofalitsa uthenga wabwino kuposa amuna, maka chifukwa choti iwo akhoza kufikira mosavuta ana, achinyamata a zaka za pakati pa 13 ndi 19, komanso ngakhale anthu okalamba, pambali pofikira amayi anzawo. Kuthekera kwa amayi mu ntchito yopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ndi kwakukulu kwambiri.

Kufunikira kwa ntchitoyi kukutilimbikitsa kuchita zinthu izi ziwiri: **Choyamba**, mwapemphero ife tiyenera kuunguzanso miyoyo yathu ndi kuiperekanso kwa Khristu kuti tikhale ophunzira Ake oona (*Yohane 8: 31*). **Chachiwiri**, ife tiyenera kudzipereka kukhala mboni zakhama komanso anthu a chikoka chokopa ena kukhala ophunzira a Yesu. Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN lakonzedwa ndi cholinga chokwaniritsa ntchito ziwiri tatchulazi. Amayi onse amene adzatenge mbali mu utumiki wa Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN, adzakhala ndi gawo loti achite mu Utumiki Waukulu. Mulungu wasankha inu! Uwutu ndi mwayi waukulu kwa inu.

Gulu la Chikoka cha Amayi likuona kuti pali Akhristu akazi amene alimbikitsidwa kukhala ophunzira a Yesu ndi kuphunzitsa amayi anzawo ndi anthu ena kukhalanso ophunzira a Yesu amene atsimikiza kukhazikitsa gulu la zauzimu ndi amayi anzawo amene pamapeto pake nawonso adzakhale opanga ena kukhala ophunzira Ake. Tiyeni tikhale opindula miyoyo!”

Ulemerero wonse ukhale kwa Mulungu, amene chisomo Chake chili maziko a ntchito yonse yabwino m'miyoyo ya ophunzira a Khristu.

Ine wanu chifukwa cha ntchito ya Khristu,

Masomphenya a Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN



Polemba

Vesi Lotsogolera: Akolose 1:10

“Kuti mukayende koyenera Ambuye, kumkondweretsa monsemo ndi kubala zipatso mu ntchito yonse yabwino; ndi kukhala m’chizindikiritso cha Mulungu.”



Mawu Oyamba

1. Ambiri amakhulupirira mwa Yesu, koma wophunzira Wake ndi munthu amene amamkonda kwathunthu ndi kumtsata Iye.
 - a. Makamu a anthu anakhulupirira Yesu chifukwa cha chakudya, machiritso, maombedwe, ndi ufulu wa ndale. Kodi iwo analidi ophunzira a Yesu? (Yohane 6:14-15).
 - b. Atumwi khumi ndi awiri aja anadzipereka kukhala ndi Yesu ndi kumtsata m’miyoyo yawo yonse. Kodi iwo anali ophunzira Ake? (*Mateyu 4:19-20*)? Mu phunziro limeneli tipezamo makhalidwe enieni oona a wophunzira wa Yesu Khristu, ndipo ife eni tiphunzira kukhala ophunzira Ake.
2. Mu phunziro limeneli tipeza makhalidwe a wophunzira wa Yesu ndi kukhala ophunziea Ake ie eni.

Makhalidwe a Wophunzira Woonwa wa Yesu Khristu

1. Wophunzira woonwa wa Yesu amakonda Mulungu koposa china chilichonse (*Luka 14: 16-26*).
- a. Kukonda Mulungu ndi khalidwe lofunikira kwambiri m’moyo wa wophunzira wa Yesu Khristu. Sipakuyenera kukhala chikondi china chilichonse cholimbana ndi chikondi chathu cha pa Yesu Khristu. Chikondi chathu pa Yesu chiyenera kuposa ngakhale chikondi chathu pa ife eni; tiyenera kumkonda Iye kuposa zokhumba zathu, zomwe timakonda kuchita, zizolowezi zathu, nthawi yathu yopumula, komanso zisangalalo zathu.

b. Chikondi cha wophunzira wa Yesu pa zinthu zina zonse chimakhala chidani poyerekeza ndi chikondi chake pa Yesu.

- Ife tikudziwa kuti sitikuyenera kudana ndi mabanja. Mwachitsanzo, Petro analowa mu utumiki pamodzi ndi mkazi wake (*1 Akorinto 9:5*).
- Ife tikudziwa kuti tiyenera kusamalira banja ndi abale athu. Baibulo likuti iwo amene satero “aipa koposa wosakhulupirira” (*1 Timoteo 5:8*).
- Miyambo 31:10-31 akulangiza akazi kukhala okhulupirika ndi oopa Mulungu ndi osamalira pa khomo pawo. Ndime za m’Chipangano Chatsopano, 1 Timoteo 2:9-11 ndi 1 Petro 3:1-6 ndi chidule cha malangizo amene ali m’Chipangano Chakale.
- Liwu loti kuda mu Luka 14: 26 likutanthauza kukonda mochepa chabe. Ife tiyenera kukonda Khristu koposa mmene timakondera banja lathu.
- Ife tiyenera kukonda Khristu, ntchito Yake ndi Mawu Ake poyerekeza ndi mabanja athu komanso abale athu.
- Ife tiyenera kulolera kuwasiya ngati lye atatiitana kupita kukalalikira uthenga wabwino
- Ife tiyenera kugonjera lye popanda kung’ung’uza ngati atawachotsa pamaso pathu.

c. Yesu anatsindika choonadi chimenechi mu Mateyu 10: 37. Vesi limeneli liyenera kumvetsedwa kuti likuti Yesu ayenera kukonedwa koposa china chilichonse. Ngati sitingathe kutero ndiye ifetu sitikuyenera kutchedwa ophunzira Ake kapena Akhristu.

d. Wophunzira amene amamtenga Yesu monga woyamba ndi wofunikira koposa zonse m’moyo mwake adzalandira mphotho (*Mateyu 6: 33, Marko 10:28-30*).

2. Wophunzira wa Yesu amansenza mtanda wake (Luka 14: 17, Marko 8:34-35).

a. Mu mpingo woyambirira, mosiyana ndi mpingo wa lero, mtanda umaimira imfa. Ngati mkazi atasankha kukhala wophunzira wa Yesu, iye ayenera kusenza mtanda wake tsiku ndi tsiku.

b. Maganizo amenewa ndi ofanana ndi maganizo a Paulo: “Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Khristu, ndi kufa kuli kupindula (Afilipi 1:21). Mkazi wotsata Khristu ayenera kukhala wokonzeka kutaya ngakhale moyo wake chifukwa cha Khristu ndi ntchito Yake.

c. Iye ayenera kudzikhaniza yekha kuti athe kulamulira zokhumba za thupi. Wophunzira wa Yesu sayenera kufuna zisangalalo za dziko lapansi kapena chuma, koma akhale wosunga mwambo. Iye ayenera kukhala wodzikhaniza m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku ndi kulolera kupereka zake zonse nsembe, ngakhale zotonthoza ndi zosangalatsa za dziko lapansi chifukwa cha Khristu.

d. Molimba mtima ndi mokondwera iye ayenera kusenza udindo umene Mulungu wampatsa chifukwa cha ntchito Yake, pamene iye wasenzanso udindo wosamalira banja lake.

- Potero, ndi kofunikira kwa wophunzira wa Yesu kuzindikira kusiyana kwa katundu amene wasenzetsedwa ndi Mulungu ndi katundu amene iye wasenza chifukwa cha ntchito za uchimo za iye mwini kapena za ena (mwachitsanzo nkhanza).

- Wophunzira wa Yesu wasenza goli la Khristu (Mateyu 11:30). katunduyo akuoneka ngati ndi wolemera kwambiri, wophunzirayo ayenera kupemphera kuti Mulungu amupatse nzeru ndi thandizo kuti ataye akatundu amene abwera chifukwa cha machimo, ndi kumpatsa mphamvu kuti athe kusenza mosavuta akatundu amene Khristu akumuthandiza kusenza.

3. Wophunzira wa Khristu woona ayenera kudza pambuyo Pake (Luka 14:27).
 - a. Kutsata Khristu kumatanthauza kumvera malamulo Ake. Aliyense amene amakonda Khristu adzamvera chiphunzitsotso Chake. Ndipo aliyense amene amamvera malamulo Ake, amakhalabe m'chikondi Chake (*Yohane 14:23; Yohane 1:10*).
 - b. Kutsata Yesu kukutanthauza kutsatira chitsanzo Chake. Wophunzira woona wa Khristu nthawi zonse amalingalira moyo ndi ziphunzitsotso za Khristu, Iye tsiku ndi tsiku amakhala akukonza ndi kusintha moyo wake pomvera malamulo ndi kutsanza chitsanzo cha Khristu. (Afilipi 2:4).
 - c. Kutsatira Yesu kumatanthauza kudzipereka kwathunthu ku cholinga Chake. Apanso akuyenera kuchita momwe anachitira Paulo amene akuti "Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Khristu" (Afilipi 1:21).
 - d. Kutsatira Khristu zimatanthauza kukhala wokhulupirika kwa Iye kufikira imfa. Wophunzira wa Yesu amaima nji mwa Khristu m'chikhulupiriro chake, kutsimikiza kuti sadzamusiya Iye konse. Si munthu amene amangoyamba chabe kumtsata kenaka ndi kumusiya, koma iye amene amatsiriza ndi kulandira mphotho (Afilipi 3:11-14; Chivumbulutso 2:10).
4. Wophunzira woona wa Yesu ayenera kukhala wokonzeka kutaya chuma chake (Luka 14:33; Marko 10:21)
 - a. Ophunzira a Yesu si ndiwo eni ake a miyoyo yawo; iwo angokhala adindo chabe oiyang'anira miyoyoyo (1 Akorinto 6:19).
 - b. Mariya wa ku Betaniya anadzoza mapazi a Yesu ndi mafuta onunkhira bwino ndi a mtengo wapatali a nardo (Yohane 12:3).
 - c. Mnyamata mwini chuma anasoweka chinthu chimodzi: iye anakonda chuma chake koposa Yesu. Chotero, iye sakanatha kutsata Yesu (Marko 10:21-22).
5. Wophunzira woona wa Yesu amadziwa Mawu a Mulungu ndi kukhala m'Mawuwo (Yohane 8:31).

- a. Ambiri iwo amene anatsata Khristu poyamba anamukhulupirira lye, koma kenaka anamusiya (Yohane 6:6). Yesu anati, wophunzira Wake ndi iye amene amapitiriza kukhala m'Mawu Ake. Umboni woona woti ife timakonda Khristu ndiwo kupitiriza kukhulupirira m'Mawu Ake ndi kumumvera lye nthawi zonse.
- b. Wophunzira wa Yesu amafunitsitsa Mawu a Mulungu monga mmene mwana wakhanda alirira kufuna mkaka wa mayi wake (1 Petro 2:2).
- c. Wophunzira wa Yesu ayenera kudya Mawu a Mulungu kuti akhale ndi moyo-kuti akule mu uzimu ndi kugonjetsa Satana. Ife tikamadya Mawu a Mulungu timakhala kuti tikudya Khristu (Mateyu 4:4; Yohane 6:35).
- d. Wophunzira wa Khristu amasenza goli lake ndi kuphunzira kuchokera kwa lye mmene angathere, kumvera malamulo Ake ndi kukwaniritsa chifuniro Chake chomwe chavumbulutsidwa m'Mawu Ake (Mateyu 11:29- 30).
6. Wophunzira wa Khristu ndiye munthu amene amafuna kumkondweretsa lye pokhala moyo woyera (1 Petro 1:15).
- a. Mulungu waitana ophunzira a Khristu kuti iwo akhale moyo wa chiyero (1 Atesalonika 4:7).
- b. Panthawi ya kupulumutsidwa kwathu ife timapangidwa kukhala woyera mwa Yesu Khristu, ndipo tapemphedwa kukhala oyera nthawi zonse (1 Akorinto1:2).
- c. Liwu loti “chiyero” limatanthauza kuti ife tapatulidwa, talekanitsidwa ndi machitidwe a anthu osakhulupirira amene atizungulira, ndipo tadzipereka kwa Mulungu komanso ku ntchito Yake. Wophunzira wa Yesu Khristu ayenera kukhala wosiyana ndi wina aliyense yemwe si wophunzira Wake; iye amakhala wolumikizana ndi Mulungu wamoyo komanso wopatulika.
- d. Chiyero ndi umboni wa chipulumutso chochokera kwa Mulungu ndi kupezeka Kwake m'moyo wa wophunzira (2 Yohane 3: 6-9).

7. Wophunzira wa Yesu amakonda anzake (Yohane 13:34-35).

a. M'zaka zana zoyambirira chikondi cha pa abale ndicho chimene chinali khalidwe losiyanita Akhristu ndi anthu ena. Katswiri wina wolembe mbiri pofotokoza za Akhristu amenewa anati, "Iwo amakondana wina ndi mnzake ngakhale asanadzizwane." Uwu ndi umboni wawo woti iwo analidi otsatira a Khristu.

b. Ophunzira a Yesu amakondana wina ndi mnzake chifukwa iwo azindikira chikondi chachikulu chimene chaonetseredwa pa iwo mwa Yesu komanso chimene chaonetseredwa ndi Yesu.

c. Aliyense amene wakhulupirira akuti Yesu ndi Khristu wakhala mwana wa Mulungu. Ndipo aliyense amene akonda Atate akondanso ana Ake (1 Yohane 5:1).

d. Mu Chihelene muli mawu atatu otanthauza "chikondi": ndipo mawuwa ndi "eros, philo, ndi agape," Liwu limene lagwiritsidwa ntchito mu 1 Yohane, ndi loti "agape" lomwe tanthauzo lake ndi chikondi chopanda undekha kapena chikondi chosadzikonda. Ophunzira a Yesu ayenera kukondana wina ndi mnzake ndi chikondi cha Mulungu chomwe ndi chosadzikonda (1 Yohane 16-18). Izi zimapangitsa kuti pakhale chiyanjano choona chomwe chimapangitsa munthu kumva kuti ndi wotetezeka.

8. Wophunzira wa Yesu woona amabereka chipatso chochuluka (Yohane 15: 5) .

a. Mulungu ndi wosunga munda wampesa, Yesu ndiye mpesawo ndipo wophunzira wa Yesu ndiye nthambi zimene ziyenera kubala chipatso. Nthambi yomwe sibala chipatso iyenera kuchotsedwa, kutsadziwa ndipo idzatsadziwa. Kubala chipatso kwa Mulungu ndi umboni woona wosonyeza kuti Mkhristuyo ndi wophunzira wa Yesu (Yohane 15:1-2, 6).

b. Mawu oti "Mukabale chipatso chochuluka" akutanthauza kubala chipatso pochita ntchito zabwino, nthawi zonse kuchuluka mu ntchito ya Ambuye. Chikhulupiriro chathu, kutembenuka kwathu, ndi chipulumutso chathu chosatha si ntchito, koma ndi mphatso zaulere za chisomo cha Mulungu, komabe kupyolera mu kubadwanso kwathu mwatsopano, Mulungu anatilenganso mwa Khristu kuti tizichita ntchito zabwino zimene Mulungu anazipangiratu (Aefeso 2:10).

c. Wophunzira wa Yesu amaonetsera chipatso cha Mzimu
(*Agalatiya 5:22- 25*).

d. Ophunzira a Yesu amabala ophunzira anzawo, amatsogolera ena kudza kwa Khristu ndi kuwaphunzitsa kumvera zinthu zonse zimene Iye anawalamulira (*Mateyu 28:18-20*).

Mathero

1. Yesu akutiitana kuti tikhale ophunzira Ake, ndi kutinso tipange ena kukhala ophunzira Ake. Chomvetsa chisoni ndi choti si “Akhristu” onse amene ali ophunzira a Yesu.
2. Wophunzira wa Yesu ndi munthu amene amasunga mwambo; izi zikutanthauza kuti iye amachita zimene Mbuye wake akufuna, osati zofuna za iye mwini zokha.
3. Wokhulupirira wa Khristu amadziwa kuti iye ndi wogulidwa ndi mtengo wapatali ndi kutinso moyo umene iye ali nawo si wake koma wa Mulungu.
4. Yesu ndiye Mbuye wa wophunzira, kutanthauza kuti, Iye ndi amene ali ndi umwini wa wophunzira komanso kuti Mulungu yekha ndi amene amasunga moyo wa wophunzirayo.

Mafunso Okambirana

1. Wophunzira wa Yesu woona amakonda Mulungu kuposa wina aliyense komanso china chilichonse. Kodi ndi zinthu ziti m’moyo zimene zimakopa wophunzira kuti azikonde kuposa Mulungu?
2. Kodi ndi zinthu ziti zimene inu mumachitira ena kusonyeza kuti mumawakonda?
3. Kodi inu mwakangalika kubala chipatso posungitsa mwambo mwa ena? Kodi mkati mwa mwezi wathawu inu mwachitirapo umboni kwa wina ndi kupindula moyo wake kudza kwa Khristu?
Nanga ngati sichoncho, ndi chifukwa chiyani simunatero?

3

Mariya wa ku Betaniya Wophunzira wa Yesu Wabwino

Vesi Lotsogolera: Yohane 12:3



“Pamenepo Mariya mmene atenga muyeso umodzi wa mafuta wonunkhira bwino a nardo a mtengo wake wapatali, anadzoza mapazi a Yesu, napukuta mapazi ake ndi tsitsi lake; ndipo nyumba inadzazidwa ndi mnunkho wake wa mafutawo.”

Malembo amene atchula Mariya wa ku Betaniya: Luka 10:38-42; Yohane 11:1-4; Yohane 12:3-9. Malembo amene akutengedwa kuti akukamba za Mariya wa ku Betaniya koma popanda kumutchula dzina: Mateyu: 26: 6-13; Marko 14:3-9.

Njira zisanu ndi ziwiri zomwe Mariya wa ku Betaniya anationetsera za momwe tingakhalire ophunzira a Yesu abwino.

1. Mariya anali pa ubwenzi wabwino ndi Yesu

a. Mariya, Marita mchemwali wake ndi Lazaro mlongo wawo, analandira Yesu m'nyumba mwawo. (*Luka 10:38-39*).

b. Mariya anali ndi chikhulupiriro mwa Yesu. Iye anali kukhulupirira kuti Yesu anali bwenzi lawo loona loti likhoza kuwathandiza, anali ndi chikhulupiriro kuti Yesu akadatha kuwathandiza mu nthawi ya imfa iyi ya mlongo wawo (*Yohane 11:32*).

c. Mariya anakhulupirira kuti Yesu anali ndi mphamvu yaikulu, yomwe ikanakwanitsa ngakhale kulepheretsa imfa ya mlongo wake (*Yohane 11:32*). Chinthu choyamba chomwe chimafunika kuchita kuti ukhale wophunzira wa Yesu ndicho kumudziwa Iye monga munthu pawekha.

Ife timafunika kulapa machimo athu ndi kulandira Khristu m,miyoyo yathu. Ndipo chachiwiri, ife timafunika kumukhulupirira Iye.

2. Mariya anakhala pa mapazi a Yesu.

a. Mariya anakhala pamapazi a Ambuye kumvetsera zimene Ambuyeyo anali kuphunzitsa. Wophunzira wa Yesu amaphunzira Mawu a Mulungu, Baibulo, komanso amapemphera ndi kumvetsera malangizo a Mulungu (*Luka 10:39*).

b. Mariya anagwa pa mapazi a Yesu modzichepetsa pamene anakumana pa manda a mlongo wakeyo Lazaro. Mariyayo anakhulupirira kuti Mulungu anali ndi mphamvu yonse ndipo anapempha thandizo la Mulungu modzichepetsa. Wophunzira amabwera pamapazi a Yesu nthawi iliyonse ya chosowa chake kumupempha Iye (*Yohane 11:32*).

c. Mariya anadzoza mapazi a Yesu mafuta wonunkhira, nagwada kupukuta mapaziwo ndi tsitsi lake (*Yohane 12:2*).

3. Mariya anali kuonetsera chikhulupiriro chake m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku.

a. Mariya anali chiwalo cha banja lomwe linkatsata Yesu m'moyo wawo wa tsiku ndi tsiku (*Luka 10: 38-42*).

b. Kukhala wotsatira woona wa Yesu sikunapangitse Mariya kukhala wotetezeka ku chidzudzulo chopanda chilungamo chochokera kwa mmodzi wa anthu a banja lake lomwe (*Luka 10:38-40*).

c. Kukhala wotsatira woona wa Yesu sikunapangitse Mariya kukhala wotetezeka ku mavuto a moyo uno (*Onani nkhani ya Lazaro, Yohane 11:44*).

d. Kukhala wophunzira wa Yesu sikunampange Mariya kukhala wotetezeka ku chidzudzulo chankhanza kuchokera kwa anthu ena (*Mateyu 26:8-9; Marko 14:4-5; Yohane 14:4-6*).

Wophunzira wa Yesu amadzikaniza yekha ndi kuvomereza chifuniro cha Mulungu m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku ndi kukhala ndi chikhulupiriro chonse mwa Iye.

4. Mariya anadziwika ndi ntchito zake.

a. Mariya atamva kuti Yesu akumuitana, nthawi yomweyo iye anapita kumene kunali Yesu. Wophunzira amamvera nthawi yomweyo pamene wadziwa cholinga ndi chifuniro cha Yesu pa iye (*Yohane 11:28-29*).

b. Mariya anampatsa Yesu chinthu cha pamtima pake, mphatso yake ya mtengo wapatali koposa zonse. Yesu watichitira zambiri; iye ayenera kupatsidwa ntchito ndi kuyesetsa kwathu konse (*Yohane 12:3*).

c. Kumpatsa Yesu muyeso waukulu wa mafuta wonunkhira a mtengo wapatali kunalimbikitsa woperekayo, Mariya kukhala munthu wodzipereka kwambiri ku utumiki wa Khristu. Ophunzira a Yesu amadzipereka ku utumiki wa Khristu. Ife eni ndi mafuta wonunkhira a mtengo wapatali oyenera kuperekedwa m'chikondi, m'kutumikira Yesu (*Marko 12:3*).

d. Mariya anatsegula msupa yake natsanula mafuta wonunkhira chifukwa cha Yesu. Monga Mariya, ophunzira a Yesu amatsegula miyoyo yawo ndi kudzitsanula okha chifukwa cha Yesu (*Marko 14:3*).

5. Mariya anadziwika chifukwa cha moyo wake wobala chipatso.

a. Abwenzi a Mariya ankabwera kwa iye kudzakumana ndi Yesu. Ataona zimene Yesu anali kuchita iwo anakhulupirira mwa Iye. Wophunzira wa Yesu ndi munthu amene amapindula miyoyo (*Marko 11:45*).

b. Pamene Mariya anatsanula mafuta onunkhirawo pa mapazi a Yesu, nyumba yonseyo inadzazidwa ndi mnunkho wa mafutawo (*Yohane 12:3*). Khalidwe la tsiku ndi tsiku la wophunzira wa Yesu limaonetsera chipatso chokoma cha Mzimu Woyera wa Mulungu, chikondi, chimwemwe, mtendere, chifatso, chifundo, ukoma, kukhulupirika, kudekha, ndi kudziletsa (*Agalatiya 5:22-23*).

6. Mariya anadziwika chifukwa cha zimene Yesu anakamba za iye.

a. Pamene Marita, mchemwali wake wa Mariya anadzudzula Mariya, Yesu anaikira kumbuyo Mariyayo (*Luka 10:42*).

- b. Pamene Yesu anafika ku Betaniya Lazaro mlongo wa Mariya atamwalira, Yesu anapempha kukumana ndi Mariya (*Yohane 11:28*).
- c. Yesu ataona chisoni cha Mariya, Iye anagwidwa ndi chifundo nalira naye pamodzi (*Yohane 11:33, 35*).
- d. Pamene Mariya ndi banja lake anagwidwa ndi chisoni chifukwa cha imfa ya Lazaro, Yesu anawatonthoza poukitsa Lazaro mbale wawoyo (*Yohane 11:38-44*).
- e. Pamene Mariya anadzudzulidwa chifukwa chodzoza Yesu mafuta wonunkhira a mtengo wapatali, Yesu anamuikira kumbuyo (*Yohane 12:7-8*).
- f. Pamene Mariya ndi mchemwali wake Malita anapempha Yesu kupita ku nyumba kwawo, Yesu analolera kutero (*Luka 10:38-39*).
- Yesu amalandira mphatso zathu mwaulemu (*Yohane 12:2*).
 - Yesu amalandira mphatso za utumiki, ndipo Iye amatithokoza kupyolera m'kupezeka Kwake komanso madalitso Ake (*Marko 14:8; Yohane 12:2*).
 - Yesu amafuna kukhala limodzi ndi ophunzira Ake (*Yohane 11:28*).
 - Yesu amafuna kukhala m'chiyanjano ndi iwo omukonda Iye (*Luka 10:38*).
7. Mariya anadziwika chifukwa anali wokhulupirika kwa Yesu m'moyo mwake.
- a. Mariya anadzudzulidwa mwankhanza chifukwa cha kulambira kwake. Yesu adaona zimene zinachitikazo ndipo anamuikira kumbuyo (*Marko 14:4- 9*).
- b. Ulosi wa Yesu womwe Iye analosera kuti Mariya adzalemekezedwa unakwaniritsidwa. Mzimu Woyera anapangitsa kuti alembi awiri a mabuku a uthenga wabwino, Mateyu ndi Marko, onse alemba nkhani iyi ya Mariya ndi ulosi uwu wa Yesu m'mabuku awo. Onse amene amawerenga Baibulo amaphunzira za zimenezi,

komanso chifukwa cha kuyamikiridwa kwake ndi Yesu pa zimenezi (*Mateyu 26:13; Marko 13:9*). Maomboledwe a Yesu pa ife kapena mphotho yomwe angatipatse chifukwa cha ntchito zathu mwina sizimabwera mwamsanga. Mwina izi zikhoza kuchedwa kufikira titadzapita kumwamba. Komabe Iye adzathandiza ndi kulemekeza wophunzira Wake (*Mateyu 19:29*).

Mafunso Okambirana

1. Kodi ndi chifukwa chiyani kuti ine ndikhale wophunzira wabwino wa Yesu ndikuyenera kulapa machimo anga ndi kukhala pa ubale wakuya ndi Yesu? Kodi ndi zinthu ziti zimene ndingaphunzire pokhapokha ngati ine tsiku ndi tsiku ndikuyenda mu ubale wozama ndi Yesu?
2. Mariya wa ku Betaniya anali kuonetsera chikhulupiriro chake m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku? Kodi pali zochitika zina m'moyo mwanga zomwe ndiyenera kuchita bwino kuposa panopo, poleka kuyesera kulamulira moyo wanga ndekha ndi zochitika zimenezi ndi kudzipereka kwathunthu kwa Yesu?
3. Kodi ndi ntchito zapadera ziti zimene ine ndingachite zomwe zingathandize anthu ondizungulira kuona kuti ndine wophunzira wa Yesu?

Pemphero

Atate wakumwamba, Ambuye wanga wokonedwa Yesu sali pano mu umunthu kuti ndikhoza kumupatsa mphatso yomwe ndingainunkhize ndi kuikhudza monga anachita Mariya. Phunzitseni mmene ndingaonetsere kudzichepetsa kwanga ndi kubala chipatso zomwe moyo wanga uyenera kuonetsera monga wophunzira wa Yesu. Ndisonyezeni mmene ndingamakhalire kuti anthu ondizungulira athe kuona kupezeka Khristu komwe kukuonetseredwa mwa Ine. Amen.



4

Moyo wa Tsiku ndi Tsiku wa Wophunzira wa Yesu

Vesi Lotsogolera: Yohane 15: 5



“Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake.”

Mawu Oyamba

1. Mtengo uliwonse umadziwika ndi chipatso chake. Ngati ife tili ophunzira a Yesu Khristu ndi nthambi yoona ya mpesa woona, Yesu, ndiyetu izi ziyenera kuonetseredwa m’khalidwe lathu.
2. Nthawi zonse ife timayesedwa kutengera zikhalidwe ndi miyambo ya dziko lapansi. Akazi amakonda kutsanzira mavalidwe, makonzedwe ka tsitsi, nsapato, ndi zokongoletsa zina monga zibangiri pofuna kuti azioneka ngati akazi okonda za dziko lapansi. Komanso tikhoza kuyesedwa kulankhula ndi kuchita monga achitira akazi okonda za dziko. Koma Mulungu akuyembekezera kuti ife akazi amene tili ophunzira a Yesu tizikhala moyo wokondweretsa Iye.
3. Ndi chizolowezi chabwino nthawi ndi nthawi kumadzifunsa tokha mafunso amene angationetsere ngati timakondweretsa Mulungu kapena ayi pa ulendo wathu wa Chikhristuwu. Khalidwe la Mkhristu amene ndi wophunzira wa Yesu likhoza kufotokozedwa m’mitu inayi.

1. Wophunzira wa Yesu ndi chipulumutso chake.

1. Baibulo likuti, “gwirani ntchito ya chipulumutso chanu ndi mantha, ndi kunthunthumira; pakuti wakuchita mwa inu kuchita ndi kufuna komwe, chifukwa chakukoma mtima kwake, ndiye Mulungu” (Afilipi 2:12-13). **Chotero,**

a. Tikhulupirire mwa Mulungu yekha. Ife tiyenera kukhulupirira mwa Mulungu yekha kuti tipeze chipulumutso.

Kuti ife tipulumutsidwe sitikuyenera kuika chikhulupiriro chathu mu machiritso, ubatizo, ntchito zathu kapena kuyesetsa kwathu monga anthu (Machitidwe 4:12; Aefeso2:8-9).

b. Timupange Khristu kukhala Mbuye wa Moyo Wathu.

Khristu ayenera ndithu kukhala Mbuye wa miyoyo yathu.

Chifuniro chathu chiyenera kuperekedwa kwathunthu kwa Mulungu (Luka 9:23; 14:26).

2. Chipulumutso chathu chiyenera kuonetseredwa m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Chotero,

a. Tigwiritse ntchito nthawi yathu mwanzeru.

Kudzipereka kwathu kwa Khristu kuyenera kuonetseredwa mmeneu timagwiritsira ntchito nthawi yathu ndi chomwe timachiika poyamba

ndi kuchitenga monga chofunikira kwambiri m'madongosolo athu (Aefeso 5:15-16). Ife sityenera kusakasaka zosangalatsa za dziko lapansi; koma mmalo mwake ife tizigwiritsa ntchito nthawi yathu pokwaniritsa zolinga za Mulungu (Mateyu 6:33).

b. Tikhale Oyera. Mulungu anatiikira mulingo woti tikhale oyera (1 Petro 1: 15 -17).

- Ife tiyenera kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kufikira lye atasefukira kudzera kwa ife kukhudza miyoyo ya ena (Machitidwe 13: 52).

- Tsiku ndi tsiku ife tiyenera kukhala odzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti lye alamulire Moyo wathu (Aefeso (5:19).

- Tiyenera kukhala oyera m'machitidwe athu onse, mu zonse zimene timachita (1 Petro 1:13).

- Tiyenera kuyenda mwa Mzimu Woyera kuti tisakwaniritse zilakolako za thupi (Agalatiya 5: 16- 26).

c. Tikhale ndi mtima wonga wa Yesu. Mtima wathu ukhale wofanana ndi umenenso anali nawo Yesu (Afilipi 2: 5).

- Timukondweretse lye ndi maganizo oyera (Afilipi 4: 8- 9).

- Ife tiyenera kudana nalo tchimo (Masalimo 110:104).

Tikhale ndi chikhumbumtima changwirowo, podziwa kuti sitinalakwire Mulungu kapena anthu ena mwadala (Machitidwe 24:16).

- Iye tiyenera kukhala opirira ndi a chimwemwe ngakhale mu nthawi ya mavuto (Yakobo 1:2-3, 12).

11. Wophunzira wa Yesu ndi Mbuye Wake.

1. Kuti ife tikhale ndi ubale wozama ndi Mulungu, tiyenera kutenga nthawi yaitali mu pemphero:
Chotero
 - a. **Tikhale amayi a pemphero.** Tsiku ndi tsiku wophunzira wa Yesu ayenera kuyanjana ndi Mulungu m'pemphero lamphamvu (Yakobo 5:16).
 - b. **Tipemphere Kosalekeza.** Mitima yathu iyenera kukhala yolumikizana ndi Mulungu nthawi zonse (1 Atesalonika 5:17).
 - c. **tipemphere ndi mtima woyera.** Mapemphero athu ayenera kukhala okhulupirika (Mateyu 6:5-7).
 - d. **tipemphere ndi cholinga.** Tizipempherera anthu onse, maka kuwapempherera kuti apulumuke (1 Timoteo 2: 1-4).
2. Ophunzira a Yesu ayenera kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu, pokhala ndi nthawi yolowa m'Mawu Ake mozama kwambiri, Baibulo. **Chotero,**
 - a. **Tiwerege Mawu a Mulungu** (Chivumbulutso 1:3). Mawu a Mulungu ndi chakudya chamoyo kwa ife (Luka 4:4).
 - b. **Tiphunzire Mawu a Mulungu** (2 Timoteo 2:3). Izi zidzatithandizanso kuphunzitsa Mawuwo kwa ena (2 Timoteo 2:2).
 - c. **Tilingalire pa Mawu a Mulungu.**(Masalimo 1:2) Mulungu amaonjezera chikhulupiro chathu pamene tikuchita ndi Mawu Ake, kuwawerenga ndi kuwalingalira (Aroma 10:17).
 - d. **Tiloweze Mawu a Mulungu pamtima.**(Masalimo 119:11). Kubisa Mawu a Mulungu m'mitima mwathu kumatiteteza ku tchimo.

d. Tizinena Mawu a m'mavesi a Baibulo.

(Mateyu 4:1-11).

Ife tiyenera kutsatira chitsanzo cha Khristu chonena pamtima Mawu a Mulungu amene ali m'Malembo; pamene lye anati ("Kwalembedwa) kutsimikizira kuti ife timakhulupirira mu mphamvu ndi ulamuliro wa Mawuwo, maka tikakhala m'mavuto kapena m'mayesero.

e. Timvere Mawu a Mulungu (Yakobo 1:22). Malembo

onse ndi ouziridwa ndi Mulungu, ndipo ndipo ali angwiro ndi opindulitsa mmene alili mwini Wake, kuti onse amene akhulupirira ndi kumvera Mawuwo nawonso amapangidwa kukhala angwiro (2 Timoteo 3:26).

3. Wophunzira wa Yesu ndi anthu ena

I. Wophunzira wa Yesu ayenera kuonetsera chikondi cha Khristu kwa anthu onse (Marko 12:29-31). **Chotero,**

a. Onetserani chikondi kwa okhulupirira anzanu onse.

Kondanani wina ndi mnzake monga mmene Khristu amakondera inu. Umu ndi momwe ena angadziwire kuti ndinu wophunzira wa Yesu (Yohane 13:34- 35).

b. Onetserani chikondi kwa anansi anu. Ife tikaonetsera

chifundo kwa anansi athu iwo amalimbikitsika, ndipo adzazindikira kuti ndife osiyana ndi anthu ena m'dziko lino lapansili (Aroma 1:2).

c. Onetserani chikondi kwa alendo. Akhristufe tiyenera

kukonda ngakhale alendo, chifukwa timagawa kwa iwo chikondi chosefuka chimene lye anatikonda nacho potilandira monga Ake (Deuteronomo 10:19).

d. Onetserani chikondi ngakhale kwa adani anu. Ife

Akhristu tiyenera kukonda ndi kukhululukira ngakhale amene amatizunza (Luka:27- 31; Mateyu 5:44; Aroma 12:19-21).

III. Wophunzira wa Yesu ayenera kukhala mu chiyanjano ndi okhulupirira anzake (Ahebri 10:25). Chotero,

a. Khalani ochirimika kupita ku tchalitchi nthawi zonse.

Baibulo limatiuza kuti tisaleke kusunkhana pamodzi

(Ahebri 10:24 – 25).

b. Muzipita ku misonkhano ya gulu lanu komwe inu monga amayi mumaphunzitsana za utumikiwu mokhulupirika.

Gawo lina la Gulu la Chikoka cha Amayi limakhazikitsa maubale ndi amayi ena ndi cholinga chothandizana, kuphunzitsana ndi kulangizana (Tito 2:3-5).

II. Mukhale ndi chizolowezi chochereza ena, itanani

Akhristu ena ku nyumba kwanu kukacheza nawo (1 Petro 4:8-9). Ophunzira a Yesu ayenera kuonetsera makhaliidwe ofanana ndi a Khristu m'maubale awo.

Chotero,

a. Khalani munthu wosavuta kukhala ndi ena. Ife tiyenera kukhala anthu amsangala ndi achimwemwe (Afilipi 4:4-5). Izi zidzabweretsa mtendere ndi chimwemwe ku makomo athu chifukwa zimathandiza kuti tikhale limodzi ndi mabanja athu mosavuta (Aefeso 4:31-32).

b. Mukhale ndi mtima wokhululukira mwachangu.

Tiyenera kukhala omasuka kukhululukira anthu amene atilakwira (Luka 17: 3-4; Mateyu 6:14-15).

c. Pewani kukwiya pa china chilichonse.

Mkwiyo ndiwo kulingalira za zoipa zimene ena atichitira (Yakobo 3:14-18; Ahebri 12:15).

d. Mukhale ndi khalidwe lotumikira. Ife tiyenera kukhala atumiki odzichepetsa, monga Khristu (Mateyu 20:26-28); Afilipi 2: 5-8), kuonetsera chikondi cha Yesu kupyolera mu utumiki wathu kwa ena.

IV. Wophunzira wa Yesu ndi Udindo Wake Wopanga ena Kukhala Ophunzira a Yesu.

1. Nthawi zonse ophunzira a Yesu amagawana uthenga wabwino ndi anthu ena ndi kuwapatsa enawo mwayi wopeza chipulumutso. Chotero

a. Mukhale Mkhristu wochitira umboni kwa ena za chipulumutso chanu. Ife tiyenera kugawana umboni wa chipulumutso chathu ndi ena ndipo miyoyo yathu yoyera itsimikizire umboni wathuwo (Mateyu 5:16).

- b. Yesetsani kupeza mpata wogawana chikhulupiriro chanu ndi anthu ena.** Posatengera kumene muli kapena chimene mukuchita, nthawi zonse muziyesetsa kupeza mpata wogawana chikhulupiriro chanu ndi ena (Machitidwe 1:8)
2. Nthawi zonse ophunzira a Yesu ayenera kubala zipatso, pokopa ena kuti nawonso akhale ophunzira Ake. **Chotero,**
- a. Mukhale opanga ena kukhala ophunzira a Yesu** ofikirika ndi ansangala. Miyoyo yathu ikhale chitsanzo chabwino kwa ena kuti iwo atitsanze. (1 Akorinto 11:1).
- b. Mukhale omvera malamulo a Khristu kuti mupange ena kukhala ophunzira Ake.** Maitanidwe athu wopambana kwambiri koposa onse ndi woti tikwaniritse Utumiki Waukulu (Mateyu 28: 18-20)
3. Kuti tikhale anthu abwino opanga anthu ena kukhala ophunzira a Yesu ife tikufunika kukhala ophunzitsika, otha kulandira malangizo ndi kukonzedwa tikalakwitsa (Miyambo 18:15). **Chotero,**
- a. Khalani anthu ophunzitsika.** Kukonzana wina akalakwa komanso chiphunzitso zimalimbikitsa thupi la Khristu (mpingo), ndipo chidzudzulo cha umulungu ndi chifundo choyenera kuchilandira (Masalmo 141: 5)
- b. Mukhale odekha pamene mukukonza ena pa zolakwika zawo.** Kukonza wina akalakwitsa sikuyenera kuchitika mwankhanza, koma kuchitike modekha, mwaulemu ndi molangiza (Agalatiya 6:1).
- c. Mukhale wodzichepetsa pamene ena akukukonzani pa zolakwitsa zanu.** Ngati kukonzedwa kapena chidzudzulo zikubweretsa maganizo a mkwiyo, wophunzira wa Khristu ayenera kuunguza mtima wake ndi kuchotsamo tchimo kapena kunyada (Miyambo 8:13)
4. Ophunzira a Yesu abwino amamangiriridwa pamodzi ndi zingwe za chikondi kuti apitirire kukula kukhala ndi moyo wa Chikhristu chozama: **Chotero,**
- a. Ophunzira a Yesu akufunsidwa kukula ndi kusiya kukhala makanda** amene amamwa mkaka, ndipo iwo akhwime kukhala akulu (Ahebri 5:12).

b. Mudziphunzitse nokha makhalidwe abwino ndi kudzikana makhalidwe oipa kuti mukule mu uzimu. Kukula kumeneku kumadza pamene ophunzira a Yesu adzipereka kuphunzira ndi kuphunzitsa Mawu, komanso kusonkhana pamodzi ndi anzawo (Machitidwe 2: 42).

c. Mukhale okangalika kuphunzitsa gulu. Kuphunzitsana nthawi ndi nthawi kumafunika kuti wophunzira aliyense akule (1 Petro5:1- 5). Izi zimachitika potenga mbali mu gulu laling'ono la mapemphero, m'maphunziro a Baibulo, ndi pa mwambo wa kupembedza.

d. Mudzipereke ku udindo wanu monga wophunzira wa Yesu m'moyo mwanu nthawi zonse. Yesu anapemphera kuti mpingo ukhale umodzi ndi lye komanso ndi Atate. Iye timakhala amodzi pamene tikugwirira ntchito pamodzi kufika pokhwima mwa Khristu kupyolera mu kukhala wophunzira Wake wodzipereka. (Yohane 17:21).

Mathero

Baibulo limatiuza kuti munthu amaona maonekedwe akunja koma Mulungu amaona mu mtima (1Samueli 1:7). Mulungu amaona chenicheni chimene ife tili. Iye satengera kuti ife ndi atali kapena afupi, a khungu loyera kapena lakuda, ooneka bwino kapena osaoneka bwino. Chidwi Chake chimakhala pa khalidwe la momwe mitima yathu ilili. Khalidwe limeneli limaonetseredwa pamene tadziunguza tokha m'mitima mwathu mwa pemphero ndi kumufunsa Mulungu kuti lye ationetsere mmene amationera komanso ngati timamkondweretsa.

Pemphero

Mulungu Ambuye, pamene ndikuganizira zofuna kudziwa ngati ndili womvera Mawu anu komanso Mzimu Woyera, ine ndikupemphani kuti mundionetsere mbali zomwe ndikusoweka kukula. Ndiululireni tchimo langa, ndimvetsereni pamene ndikulapa, ndipo mudiyeretse kundichotsera chosalungama changa chonse. Amen.

Mdandanda wa Mbiri ndi Mafunso Oti Mudzifunse



Pezani malo a bata pomwe mukhale mulipo nokha ndipo mutatenga Baibulo lotsegula m’manja mwanu inu muwerenge ndime zotsatirazi ndi kuyankha mafunso amene akutsatira ndimezo,

Y zikusonyeza kuti “inde” ndipo pamene alembapo N zikusonyeza kuti “ayi”

Y N 1. Kodi ndimakhulupirira mwa Khristu yekha ku chipulumutso changa? (Yohane 3:16, Aefeso 2:8-9).

Y N 2. Kodi Yesu ndiye Mbuye wanga? (Luka 9:23, Luka 14:26).

Y N 3. Kodi zomwe ine ndimazitenga monga zofunikira kwambiri zimakondweretsa Mulungu? (Mateyu 6:33).

Y N 4. Kodi ine ndimalamuliridwa ndi Mzimu Woyera ndi kuyenda mwa Iye? (Galatiya 5: 16-26, Aefeso 5:18).

Y N 5 . Kodi Mulungu amakondwera ndi maganizo a moyo wanga? (Afilipi 4:8- 9)

Y N 6. Kodi ine ndimadanadi ndi tchimo? (Masalmo119:104)

Y N 7. Kodi chikumbumtima changa ndi chopanda nkhawa? (Machitidwe 24:16)

Y N 8. Kodi ine ndimapirira mavuto ndi maganizo odekha komanso okondwa? (Yakobo 1:12)

- Y N 9. Kodi Mulungu ndi wokondwa ndi moyo wanga wa pemphero? (Afilipi 4: 6; 1 Timoteo 2:1-4)
- Y N 10. Kodi ine ndimaloweza pamtima Mawu a Mulungu, kuwawerenga ndi kuwamvera (2 Timoteo 2:2, 2:1, 3:16)
- Y N 11. Kodi ine ndimakonda Mulungu komanso mnansi wanga monga mmene Khristu wandikondera (Yohane 14:34)
- Y N 12. Kodi ine nthawi ndi nthawi ndimakhala mu chiyanjano ndi gulu la okhulupirira a Chikristu? (Ahebri 10: 2)
- Y N 13. Kodi ine ndi munthu wokondwa mwachitsanzo, munthu wokhala ndi anthu ena mosavuta? (Aefeso 4:31- 32)
- Y N14. Kodi ine ndili ndi mtima wokhululuka, komanso wolandira ndi kupereka momasuka? (Mateyu 6:14-15)
- Y N 15. Kodi ine ndiwokwiya ndi kanthu kena? (Ahebri 12:15)
- Y N 16. Kodi ine ndili ndi khalidwe lotumikira? (Mateyu 20:28)
- Y N 17. Kodi ine ndikuchitira umboni, kuperekera umboni wa Khristu m'moyo wanga? (Machitidwe 1: 6)
- Y N 18. Kodi ine ndikokopa anthu ena kuti atsate Yesu? (Mateyu 28: 18-20)
- Y N 19. Kodi ine ndi wophunzitsika? (Miyambo 18:15)
- Y N 20. Kodi ine ndi kuphunzitsidwa kukhala wophunzira waYesu kapena kupatsidwa ndi munthu wina upangiri wokhudza zochitika zokhazikika? (1 Petro 5:1-5)

5

*Mwa Khristu Phungiro la Chitsanzo
Lophungitsa Kukhala Moyo Woyera*

Vesi Lotsogolera: 2 Akorinto 5:17



“Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano.”

Malembo oyenera kuwerenga: Akolose 2:9-12; Aroma 8: 5-11. Zipangizo zomwe zikufunika: mbale yagalasi yaikulu, tambula ya galasi yaing’ono, Miyala (waukulu, waung’ono, ndi wokongola yomwe ingakwane mu tambulayo), mchenga ndi dothi pang’ono.

Ndondomeko yoti mutsatire: Mudzaze m’mbale ya kalasiyo ndi madzi kuti tambula yagalasiyo imire.

Kufunikira kodzaza; kupanda pake koyesera kukhala moyo wa chiyero kunja kwa Khristu (Aefeso 5:18)

1. Ine ndinamva ndi kuwerenga zokhudza kudzaza kwa Mzimu Woyera ndipo ndinafunitsitsa lye atandizaza. Ine ndinayenera kukhala ndi mapemphero anga a mmawa (viikani tambulayo m’mbale ija kuti tambulayo idzaze madzi), koma pofika 12 koloko masana ndikumva kuti ndangodzazidwa ndi Mzimu kwatheka chabe. (Mugwedeze tambulayo kuti madzi ena ataikemo.)

Pamene mavuto ndi mayesero anadza ndinamva kuti Mzimuyo akucheperachepera mwa ine (pitrizani kutaya madzi a m’tambulamo). Mupitirizebe kutaya madzi a m’tambulamo

2. Ndinawerenga Aefeso chaputala 1 momwe akukambamo za kukhala mwa **KHRISTU**.

Mwa Khristu: kudzazidwa, chiteze; khalidwe la moyo wa Khristu. (Agalatiya 2:20).

(Ikani tambula mu mphika waukulu wodzaza madzi, ndipo tambulayo imire m'madzimo). Tsopano madziwo akudzaza mu tambulayo ndipo iyo yamira m'madzimo. (Mfunseni munthu wina kuti akhudze tambulayo popanda kukhudza madziwo).

Nthawi yomwe ife tili mwa Khristu, Satana sangathe kutipeza. (Uzani munthuyo asadabuze tambulayo koma ili chimirire m'madzimo). Kodi madzi m'tambulamo akutaika? (Muuzeni munthuyo akhutchumule tambulayo koma ili m'madzi momwemo). Poyamba, pamene tambulayo inali isanai-kidwe m'madzi komanso itachotsedwamo, titaikhutchumula madziwo anataikamo, koma tsopano pamene ikadali m'madzi momwemo iyo ikadali chidzazire!

(Mukachotsa tambula ya galasiyo m'madzimo muidzaze ndi miyala yaikulu [kuimira, machimo ooneka ndi maso amene munthu anawachita iyeasanatembenuke]. Onani Aroma 5: 6-8).

Funsani: Kodi tambula ya galasiyo ndi yodzaza? Inde, iyo ndi yodzaza madzi, koma sinadzaze ndi madzi okha, chifukwa miyalayomwe yaikidwa m'tambulamo ikukankha madzi ndi kutenga malo a madziwo. Anthu ena akukhala miyoyo mmene tchimo (miyala) likuwalepheretsa kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. **(Onjezerani miyala ina yaing'ono m'tambula yagalasiyo.)** Machimo ena amakhala ang'ono, ndiponso ena amakhala obisika ndi osadziwika kwa anthu (1 Yohane 1:8, 10; Luka 11:24-26).

(Onjezerani mabo agalasi okongola m'tambulamo). Mabowo akuimira machimo amene amakhala "ooneka okoma," makhalidwe amene ndimasangalatsidwa nawo kuwachita ndipo sindifuna kuwasiya (1 Akorinto 9:12). Machimo ena ndi machimo "ochedwetsa." Izi zikhoza kukhala zinthu zimene timazona

Tchimo limatenga malo a Mzimu Woyera; tambula ya galasiyo ikusefukira ndi madzi koma sinadzazidwe ndi madzi okha (Ahebri 12:1).

Yakobo 2:10
1 Yohane 1:9

monga zinthu zabwino, monga ndalama, nthawi kapena zisangalalo. Koma ngati tingazikonde mopyola muyezo ndi kuzigwiritsa ntchito molakwika, izo zikhoza kutibwezera m'mbuyo (Ahebri 12:1-2). Ndi chiyani chomwe chili mu mtima mwanu chimene chikutenga malo a Mzimu Woyera? Nanga ndi chiyani chomwe chadzaza mu mtima mwanu, tchimo (miyala) kapena Yesu? Madziwo akhoza kuoneka ngati ndi wodzaza kwambiri, chikhalirecho zikhoza kuthekanso kuti madzi m'tambulamo angokhalamo theka chabe.

4. (Muchotse miyalayo m'tambulamo ndipo muidzazenso ndi madzi. Muike dothi pang'ono m'madzimo. Funsani munthu wina kuti amwe madziwo).

Ngakhale dothi litakhala lochepa limao-nonga madzi onse, chotero ngakhale tchimo litakhala lochepa nalonso limaononga munthu yense. Mulungu amatiuza kuti tikhale angwiro monganso Atate wathu wa kumwamba ali wangwiro. (Mateyu 5:48).

Chomwe chili
mkati chimatuluka
(Yakobo 3:9-12).

5. (Musiye tambula ya galasiyo m'madzi momwemo ndipo muyesere kutayamo madzi ena.) Pamene ndasiyabe tambulayo m'madzi momwemo ndi kutayamo ena, kodi ndi chiyani chimene chikutuluka kuchokera m'tambulamo? Ndithudi m'tambulamo mukutuluka madzi. Ngati wina atakukwiysani, kodi ndi chiyani chimene chimatuluka pakamwa panu? Kodi ndi matemberero kapena madalitso? Komatu pakamwa pa Yesu panali kutuluka madalitso." Atate muwakhulukire iwo." Kodi ili ndi yankho lomwe ndimayankha nthawi zonse kwa mwamuna kapena mkazi wanga iye akakwiya, ana anga amene akundipempha kanthu kena, wogulitsa mu shopu wina wamwano, dalaivala wina woyendetsa galimoto mosasamala? Ngati ndili ndi tchimo mu mtima mwanga, mkwiyo

Pamene ife
takankhidwa, ena
adzadalitsidwa
Genesis 12:1-3
1 Akorinto 1:27
Aroma 12:1- 2

udzatuluka mwa ine monga vinyo wosasa. Ngati ndili wodzazidwa ndi Khristu, Iye yekha ndi yemwe adzatuluke mwa ine ngati uchi wozuna!

6. (Mukweze tambula yodzaza madziyo pafupi ndi munthu wina ndipo mumufunse kuti amenye tambulayo. Muonetsetse kuti madzi ena a m'tambulamo ataikira pa munthuyo.)

Mu zochitika zonse zokhudza kulumikizana komwe komakhalapo m'maubale, munthu yemwe inu mukulumizana naye ayenera kukhudzidwa ndi chikoka cha Mzimu Woyeramene ali m'moyo mwanu. Munthuyo ayenera kumva kuti iye ndi wodalitsika pokhala pafupi nanu, ngakhale atakukwiwitsani. Kodi inu mwakhala mukulankhula zotani kwa anthu ena?

Tangoyerekezani kuti moyo wanu ndi botolo; taliponyerani m'nyanja ya Mzimu wa Mulungu ndi kumulola Iye kuti alikumbatire ndi kulidzaza. Mupereke moyo wanu kwa Khristu, ndi kumulola Iye akudzazeni, akuyangateni, akukumbatireni ndi kukhala mwa inu (Yohane 17:1- 26).

Mafunso Okambirana:

1. Kodi ndi "machimo ati ang'ono ang'ono ooneka okoma" amene inu mukuyesedwa nawo?
2. Ndi chiyani chimene "chimatuluka" m'moyo mwanu wina akagundani?

Pemphero

Vomerezani machimo anu ndi mawu a mkamwa mwanu, mufunseni Khristu akuthandizeni kudziwa miyala ndi dothi zomwe zili m'moyo mwanu, mufunseni Iye akuchotsereni zimenezi, ndipo mudzipereke kwathunthu kwa Iye amene ali mwa inu, yemwe ndi chiyembekezo cha ulemerero (1 Akorinto 1:27).

6

Wophunzira wa Yesu ndi maubale ake.

Vesi Lotsogolera: Aroma 12:18



“Ngati nkutheka, monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse.”

Mawu Oyamba

1. Ngakhale zili zovuta kwa ife kumvetsetsa zokhudza Mulungu, tiyenerabe kudziwa kuti Iye ndi Mulungu mmodzi mwa atatu, ndipo atatuwo ndi: Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Koma pa nthawi yokhayokhayo Iye ali Mulungu mmodzi (Deuteronomo 6:4).
2. Atatu a Utatu wa Umulungu amakhala pa ubale wamphamvu nthawi zonse. Momwemonso, ophunzira a Yesu ayenera kukhala mu ubale wamphamvu ndi anthu ena nthawi zonse.

Mitundu Inayi ya ya Maubale Yomwe Wophunzira wa Yesu Ayenera Kuisamalira

1. Mkazi amenenso ndi wophunzira wa Yesu ayenera kusamalira ubale wake ndi mwamuna womanga naye banja (ngati iye ali pabanja).
 - a. Kumbukirani kuti mmene zonse zikhalira m'moyo wa wophunzira wa Khristu, ukwati wa wophunzira wa Yesu uyenera kupereka ulemu ndi ulemerero kwa Mulungu (1 Akorinto 10:31)
 - b. Baibulo likulangiza akazi kumvera amuna awo a iwo eni monga mmene iwo amvera Ambuye. Kumvera kumeneku

Mawu otengedwa m'buku lotchedwa
He Married a Princess, (Anakwatira Mwana wa Mfumu)
Iolembedwa ndi Thelma Braun

- Mwamuna ndi mkazi amene amakonda Mulungu koposa china chilichonse m'miyoyo yawo, ndipo koposa mmene iwo eni amakonderana, komanso amene amaphunzira Mawu Ake pamodzi ndi kumapempherera limodzi, adzakhala ndi mphamvu Yake yaikulu yogonjetsa mtopola uliwonse wochokera kwa mdaniyo (Satana).
- Ngati nthawi zonse inu mumaonetsera khalidwe la msangala, panyumba panu padzakha malo a chimwemwe.
- Phunzirani kuyamikira mwamuna wanu nthawi zonse. Mwano ndi khansa yoononga kulumikizana kwanu ndi mwamuna wanu.
- Musakhale ndi chizolowezi chokhumudwitsana nthawi zonse. Nthawi zonse yejetsani kulimbikitsana.
- Limbikitsani mwamuna wanu. Mukondeni. Mumusunthire chifupi ndi Mulungu, chifukwa iye sadzakhala wanu kwathunthu koposa momwe angakhaliye wa Mulungu kwathunthu!
- Pamene Khristu anatilamula kokondana wina ndi mnezake, kodi iye anaonjerapo kuti tisakonde azilamu athu?
- Mwamuna ndi mkazi a pabanja amene amakhala ndi Mulungu komanso amakhala chifukwa cha Mulungu, chuma chawo ndi chisangalalo chawo zimakhala zikukulirakulira mkupita kwa nthawi. Ndipo apatu mfundo yofunikira ndi kukhala mwa Mulungu. Pamene pali Mulungu palibe chomwe chingakhale champhamvu koposa banja. Banja lopanda Mulungu silingalimbe ayi. Langizo lofunikira kwambiri ku mabanja onse ndi loti, banja lililonse liyenera kukhala chifupi ndi Mulungu.

ndi kumvera mwamunayo, kulemekeza ndi kumvera ulamuliro wake molingana ndi lamulo la Mulungu (Aefeso 5:22,25).

Khalidwe lofanana ndi la Khristu la mkazi amene ndi wophunzira Wake likhale la chikoka chabwino pa mwamuna amene wamanga naye banja ngati mwamunayo ali wosatembenuka. Mawu a chihero, odzichepetsa, oopa Mulungu ndi a chikondi amene mkaziyo akulankhulana ndi mwamuna wakeyo, mophatikizana ndi chipatso cha Mzimu, zikhoza kutembenuza mwamunayo, osati mwa iye yekha koma ngakhalenso mwa Yesu Khristu, Mbuye wake. “Momwemonso, akazi inu, mverani amuna anu a inu nokha; kuti, ngatinso ena samvera mawu, akakodwe opanda mawu mwa mayendedwe a akazi.”(1 Petro 3:1).

d. Mkazi amene ndi wophunzira wa Yesu akhoza kukhala wodzikhulupirira kupyolera mu cholinga chabwino chomwe Mulungu wamukonzera mu udindo wake monga mkazi wa pabanja: “womthangatira iye” (Genesis 2:18). Mkazi wabwino amakonda mwamuna wake (Tito 2:4) komanso “mkaziyo amchitira zabwino, si zoipa masiku onse amoyo wake” (Miyambo 31:12).

e. Ukwati wa Chikristu ndi mwayi kwa okhulupirira wotumikira chisomo ndi chikondi cha Mulungu kwa omanga naye banja. Ngati onse, mwamuna ndi mkazi ali okhulupirira, onse pamodzi ndi “olowam’nyumba pamodzi wa chisomo cha moyo” (1 Petro3:7). Iwo si oyanjana kuthupi kokha, koma ali oyanjananso m’moyo wosatha. Iwo amasunga ubale wawo ndi mumgwirizano uwu wauzimu popewa kuti pasakhale kukangana kapena kusakhutitsidwa kwina kulikonse, kapena pothetsa zonsezi kupyolera m’kukambirana. Izi ndi zofunikira kuti munthu akhale ndi moyo wa pemphero ndi wopanda zopinga (Marko 11:25).

f. Ndi chinthu chofunikiranso kwambiri kukhala ndi nthawi yocheza ndi womanga naye banja, nthawi yomwe tingachezerane mwakuya kwambiri. Ubale wamphamvu chotere ndi chinthu chotiteteza ku mayesero. (1 Akorinto7:3- 5).

g. “Mulungu anakhazikitsa banja; ilo ndi chikonzero Chake, ndipo lye amalikonda. Aefeso 5: 22-23 akusonyeza kuti ubale wa mwamuna ndi mkazi omwe ali pabanja ndi phunziro la chitsanzo lotionetsera mmene Khristu amaukondera mpingo.

Iye amafuna kuti banja likhale chikhazikitso chopatuliika, chokongola, chithunzi chounikira dziko lonse lapansi, choonetsera chikondi Chake changwiwo ndi chopanda chodetsa pa mkwatibwi Wake (mpingo).”- Mama Thelma Brawn.



2. Wophunzira wa Yesu ayenera kulemekeza ndi kusamalira ubale wa pakati pa iye ndi ana ake.

a. Aefeso 6:4 akutipatsa zomwe ife monga makolo tiyenera kuchita ndi kutiletsa zomwe sitienera kuchita: musakwiyitse ana anu. Muwalere m'maphunziro, m'chilamulo ndi m'malangizo a Ambuye.

b. Makolo akhoza kukwiyitsa ndi kupsetsa mtima ana awo pokhala kholo lovuta pa china chilichonse, lotchingira mwanoyo pa china chilichonse, lokwiya pa china chilich onse, lokonda mwana wina kwambiri mosiyana ndi anzake, ndipo ngakhale lochita ndi anawo mosiyana. (Yakobo 1:2-8).

c. Makolo ayenera kuonetsera khalidwe la Mulungu mu ubale wawo ndi ana awo (chimodzimodzinso ndi wina aliyense). Ife tiyenera kukhala a chikondi ndi a chifundo, monga Atate wathu wa kumwamba. (Aefeso 4:32).

d. Ife tiyenera kupereka tizilango kwa ana athu mwachikondi ndi cholinga chofuna kusungitsa mwambo pa anawo monga mmene Mulungu Atate wathu achitira ndi ophunzira Akefe (Ahebri 12: 6).

e. Miyambo 22: 6 akuti “phunzitsa mwana poyamba njira yake. . .” Liwu loti phunzitsa ndi liwu lomwe limathanthauza kuphunzitsa komwe kukuphatikizira chilango chosungitsa mwambo mwa munthu.

f. Tiyenera kuletsa (liwu lomwe ndi gwero komwe liwu loti kuletsa linatengedwa limathanthauza kuphunzitsa, kukonza, ndi kutsutsa ana athu iwo akalakwa.) Mu 1 Samueli 2:34- 35 tikuwerengamo kuti Eli sadaletsa ana ake, ndipo Mulungu analola kuti anawo aonongedwe ndi adani awo.

g. Ndi chinthu chofunikiranso kwambiri kukhala ndi nthawi yocheza ndi ana athu-nthawi yomwe timalumikizana nawo mwakuya ndi mowirikizawa (Luka 1:17).

3. Wophunzira wa Yesu ayenera kulemekeza ndi kutengulira ubale wake ndi ziwalo za banja lake.

a. Wophunzira amakhala pa ubale wabwino ndi azilamu ake. Rute ndi chitsanzo chabwino cha nkhani imeneyi. Iye anali kukonda amayi a mwamuna wake (apongozi ake akazi) ngakhale mu nyengo zovuta-ngakhale mu nthawi yomwe iye anali ndi mwayi womasuka kulekana ndi apongozi ake. Iye sanangoganizira za ubwino wa iye mwini wokha koma anasamalanso za apongozi akewo. Iye anachita motero chifukwa anali wokhulupirira ndi woopa Mulungu wamoyo (Rute 1:16 -17); Rute 2:14, 18).

b. Wophunzira wa Yesu amasamalira banja lake kuphatikizapo antchito ake. Pofuna kukwaniritsa maudio ake a banja, iye amadzuka m'mawa kwambiri ndipo sagona msanga kufikira atamaliza ntchito zake. Iye amagwira ntchito molimbika, amakhudzika ngakhale ndi khalidwe la anthu a pabanja pake (Miyambo 31:15- 27).

c. Wophunzira wa Yesu amasunga ubale, amakhala monga chitsanzo komanso mulangizi wolangiza zinthu zabwino kwa akazi achichepere poyerekeza ndi iye (Tito 2:3). Pa chifukwachi, iye amapewa khalidwe lonyoza ena, zomwe zikutanthauza kuti iye ndi munthu amene amalamulira lilime lake (Yakobo 3: 5 – 6, 8). Iye amaonetsera khalidwe lodziletsa ndi laulemu kwa anthu onse.

d. Wophunzira wa Yesu amaphunzira kuchokera m'Mawu a Mulungu kukuza khalidwe loopa Mulungu mwa iye mwini (1 Petro 1: 5- 6). Khalidwe limeneli lidzaonetseredwa m'maubale ake onse.

4. Wophunzira wa Yesu ayenera kulemekeza ndi kukhala wosamalitsa za ubale wake ndi anthu ena amene si ziwalo za banja lake.

a. Iye ayenera kuchita mwanzeru ndi anthu amene si okhulupirira Mulungu (Akorinto 4: 5). Iye ayenera kuonetsera khalidwe labwino pakati pawo, iye ayenera kukhala munthu wodzisungira ulemu ndi wokhulupirika kuti iwo asapeze chifukwa chonyozera Chikhristu. Izi zidzampatsa mpata wogawana nawo uthenga wabwino.

Mkazi amene ndi wophunzira wa Yesu ayenera kuonetsera khalidwe labwino pakati pa anthu ena, iye ayenera kukhala munthu wodzisungira ulemu komanso wokhulupirika kuti iwo asapeze chifukwa chonyozera Chikhristu. Izi zidzampatsa mpata wogawana uthenga wabwino ndi anthuwo.

b. Iye akhale wochereza anthu- womasuka kupezera ena zosowa zawo, maka iwo amene akutumikira ndi kuvutika chifukwa cha Khristu (Aroma 12:13).

c. Iye ayenera kukhala wachifundo kwa osauka ndi osowa, maka kwa iwo amene ali ziwalo za mpingo (1 Yohane 3:17; Yakobo 2:15).

d. Iye ayenera kulemekeza utsogoleri womwe uli mu mpingo wa Mulungu, kumvera machenjezo ndi ziphunzitso za atumiki a Mawu a Mulungu, amene akulalikira mokhulupirika chilangizo chonse kuthandiza iye pa Chikhristu chake (Ahebri 13:17).

e. Ngati atakhala kuti akugwira ntchito ku kampani kapena bungwe la chikunja, iye ayenera kulemekeza ndi kumvera mabwana ake. Iye ayenera kukhala wokhulupirika mu ntchito zake ngati akugwirira ntchitoyo Ambuye (Aefeso 6:5-8). Iye amvere zokhazo zimene sizili zosemphana ndi chikhulupiriro cha Chikhristu komanso Mawu a Mulungu.

Nawa mawu ena okamba za mmene tiyenera kuchitirana wina ndi mnzake otengedwa m'Chipangano Chatsopano amene akutiiza mmene tingamachitirane wina ndi mnzake mu njira yokondweretsa Mulungu:

KONDANANI WINA NDI MNZAKE:

1. Yohane 4:7 - Tikondane wina ndi mnzake
2. 1 Petro 4:8 - Mukhale nacho chikondano chenicheni mwa inu nokha
3. 1 Petro 1:22 - Mukondane kwenikweni kuchokera mumtima
4. 1 Petro 3:8 - Khalani nonse a mtima umodzi
5. Aroma 12:10 - M'chikondano cha anzanu wina ndi mnzake, mukondane ndi chikondi chenicheni
6. Agalatiya 5:13 - Mwachikondi chitiranani ukapolo

MULEMEKEZANE WINA NDI MNZAKE

7. Yohane 13:14 - Inunso muyenera kusambitsana mapazi wina ndi mnzake.
8. 1 Petro 5:5 - Koma nonsenu muvale kudzichepetsa kuti mutumikirane.
9. Afilipi 2:3 - Yense ayese anzake omposa iye mwini.
10. Aefeso 4:2 - Ndi chifatso ndi kuonetsera chipiriro ndi kulolerana wina ndi mnzake.
11. Aroma 15:7 - Mulandirane wina ndi mnzake monganso Khristu. anakulandirani inu.
12. Aroma 12:10 - Mutsogolerane ndi kuchitira mnzake ulemu.
13. Aefeso 5:21 - Mumverane wina ndi mnzake.
14. Afilipi 2:4 - Yense apenyerekeno za mnzake.
15. Marko 9:50 - Khalani ndi mtendere wina ndi mnzake

MUKHULULUKIRANE WINA NDI MNZAKE

- Aroma 14:13 - chifukwa chake tisaweruzanenso wina ndi mnzake.
17. Aefeso 4:32 - Mukhalirane okoma wina ndi mnzake, a mtima wachifundo, akukhululukirana nokha.
18. Akolose 3:13 - Mulolerane wina ndi mnzake, ndi kukhululukirana inu nokha.
19. Aroma 12:14-16 - Dalitsani, kondwani, lirani, mukhale nawo mtima umodzi wina ndi mnzake.

MULIMBIKITSANE WINA NDI MNZAKE

1. Atesalonika 5:11 - chenjezanani
21. 1 Atesalonika 5:11 - Mangiriranani wina ndi mnzake
22. Aroma 14:19 - Tilondole zinthu za mtendere ndi zakulimbikitsana wina ndi mnzake.
23. Agalatiya 6:2 - Nyamuliranani zothodwetsa
24. Akolose 3:16 - Mu nzeru yonse ndi kuphunzitsa, ndi kuyambirana eni okha.
25. Ahebri 10:24 - Tiganizirane wina ndi mnzake kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino.
26. 1 Petro 4:10 - Mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a chisomo cha mitundumitundu cha Mulungu.
27. Ahebri 3:13 - Dandauliranani nokha tsiku ndi tsiku.
28. Afilipi 1:4 - Nthawi zonse ndi pembedzero langa la kwa inu nonse ndichita pembedzero ndi kukondwera.

ZOTI MUSAMACHITE

- Yakobo 4:11 - Musamanenerana, abale.
30. Agalatiya 5:15 - Musamalumana ndi kudyana mungaonongane.
31. Agalatiya 5:26 - Tisakhale odzikuza, outsana, akuchitirana njiru.
- Yakobo 5:9 - Musaipidwe wina ndi mnzake.
33. Akolose 3:9 - Musamanamizana wina ndi mnzake.
34. Aroma 14:13 - Munthu asaike chokhumudwitsa pa njira ya m'bale wake.

7

Wophunzira wa Yesu ndi Ntchito Yopindula Miyoyo

Vesi Lotsogolera: Miyambo 11:30



“Ndipo wokola mtima ali wanzeru.”

Chaputala ichi cha buku lothandiza akazi a m’Gulu la Chikoka cha Amayi pa udindo wawo monga ophunzira a Yesu, ndi kasakaniza amene wapangidwa poika pamodzi mitu ingapo yochokera m’buku lotchedwa “Seven-Step-Soul-Saving-Seminar” lolembedwa ndi Theima Brawn, amene amatchedwa “**Mama**” ndi amayi omukonda, amene ankawalimbikitsa mu India.” Kuti mudziwe zambiri zokhudza “**Mama**” ndi chilimbikitsa chimene iye ankapereka kwa onse omudziwa, onani tsamba lomwe pali za Kupereka Ulemu ndi Zothokoza.

Bukuli likuphunzitsa njira za kuchitira umboni ndi kupindula miyoyo, ndipo maphunziro asanu ndi awiri amene ali m’bukuli amatchedwa “makwerero.” M’bukuli muli maphunziro asanu. Phunziro loyamba likutsindika pa zifukwa zimene zimapangitsa kuti kupindula miyoyo kukhale chinthu chofunikira, ndipo anayi enawo akufotokoza za njira zabwino zomwe zingathandize ntchito yofalitsa uthenga wabwino kukhala yopambana.

1

ZIFUKWA ZIMENE ZIMAPANGITSA KUTI KUPINDULA MIYOYO KUKHALE CHINTHU CHOFUNIKIRA

Anthu ochepa okha ndi amene aitanidwa kukhala alaliki, koma Mkhristu aliyense wobadwanso mwatsopano waitanidwa kukhala wopindula miyoyo. Muyenera kutsogolera anthu anu kulowa nawo m’chimwemwe chopindula miyoyo.

“Kupindula miyoyo ndi ntchito yeniyeni, yotsogolera munthu weniweni kulandira Mpulumutsi weniweni, pa nthawinsu yeniyeni.”

Billy Sunday

Zifukwa Zokhalira Wopindula Miyoyo

1. Kufunika kwa moyo (Marko 8:35-38).
2. Mfundo yofotokoza zokhudza gehena (Luka 12:4-5).
3. Masautso a Khristu pamtanda chifukwa cha wochimwa aliyense (1 Petro 3:18).
4. Kupanda pake ndi kupusa kwa dziko lapansi (1 Petro 1:24-25).
5. Khumbo la munthu lofuna kukakhala ndi banja lake lonse kumwamba (1 Atesalonika 4:16-17).
6. Ulemerero wa kumwamba (Yohane 14:2-3).
7. Mphotho zimene zikuperekedwa kwa wopindula miyoyo aliyense (Danieli 12:3).

Zofunika pa Mtumiki Monga Munthu Payekha

1. Iye mwini ayenera kukhala munthu wopulumutsidwa komanso wotsimikizika pa chipulumutso chake (2 Petro 1:10-11).
2. Iye ayenera kukhala moyo wa chiyero (2 Petro 3:14).
3. Iye ayenera kugwira ntchito mwa chikondi (1 Petro 1:22-23).
4. Iye ayenera kukhala munthu wodziwa Baibulo ndi mmene angaligwiritsire ntchito (2 Timoteo 2:15).
5. Iye ayenera kukhala munthu wokonda kupemphera (Aefeso 6:18).
6. Iye ayenera kukhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera (Aefeso 5:18).
7. Iye ayenera kukhala munthu wochitira chifundo miyoyo yotaika (Yuda 23).

Mafunso Okambirana:

Kodi ndi chifukwa chiyani zofunika zimene zalembedwa m'mwambamuzi zili zofunikira?



MMENE MUNTHU ANGACHITIRE UMBONI

Mbuye wathu safuna wina atayike, koma kuti onse akafike ku kulapa (2 Petro 3:9b). Khumbo la Mulungu ndi loti munthu aliyense akhale ndi mwayi womva uthenga wabwino. Pokumbukira zimenezi, wokhulupirira aliyense ayenera kukhala wokonzekeratu kuchitira umboni ngati Mulungu atamupatsa mwayi wotero.

Mmene Munthu Angachitire Umboni

1. Munthu amene ali mboni ya Khristu, ayenera kukhala wopulumutsidwa iye mwini (Aroma 5:9-11).
2. Fotokozani nthano ya kutembenuka mtima ndi kusinthika kwa moyo wanu (Masalimo 51:12-13).
3. Munene za mayankho amene Mulungu anakupatsani, poyankha mapemphero anu (Masalimo 50:15).
4. Mufotokoze za kukhutsidwa kwanu kwathunthu mwa Khristu (Masalimo 107:8-9).
5. Fotokozani za chipambano chanu monga munthu chogonjetsa tchimo ndi mayesero (1Yohane 5:4-5).
6. Fotokozani za mavesi a pamtima panu ochokera m'Baibulo, ndi mmene Mulungu walankhulira nanu mmawa uno kuchokera m'ndime ina yake m'Malembo.
7. Apatseni abwenzi anu uthenga wabwino wa Khristu. Muwauze za lye (Aroma 1:16).
8. Aitaneni abwenzi anuwo kuti abwere adzaone (Yohane 1:29-51).
9. Mutsateni Yesu (Mateyu 4:12-27; Marko 1:16-20).

Zolepheretsa Munthu Kuchitira Umboni Khristu

1. Mantha a Munthu (2 Timoteo 1:7; 1 Yohane 4:18; Afilipi 4:13).
2. Manyazi (2 Timoteo 1:8).
3. Moyo wa chidetso ndi wosalungama (1 Yohane 1:9)
Dziwani izi: Werengani Ezekieli 33:8 kuti mudziwe kuipa kolephera kuchitira umboni!

Mukonze Umboni wa Inu Mwini

Chimodzi cha zida zamphamvu kwambiri zochitira umboni ndicho umboni wonena za ubale wanu ndi Khristu ndi momwe ubalewo wasinthira moyo wanu. Munthu wakungu atachiritsidwa, anachitira umboni kwa atsogoleri a chipembedzo, “Chinthu chimodzi ndichidziwa, popeza ndinali wosaona, tsopano ndipenya” (Yohane 9:25b). Anthu ena akhoza kutsutsa Malembo, akhoza kutsutsana ndi chiphunzitso, kapena ganizo lina lochokera m’Malembomo, koma ndi kovuta kwambiri kukana umboni wa munthu amene moyo wake kwasinthidwa ndi Khristu.

Magawo a Umboni wa Inu Mwini

1. Fotokozani za mmene moyo wanu unalili kale musanatembenuke, musanakhale Mkhristu. Mufotokoze mmene unalili moyo wanu musanadze kwa Khristu, kwambiri mukhazikike pa maganizo anu omva ngati ndinu wopanda pake ndi wopanda chiyembekezo, omwe amakhala maganizo owanda kwambiri pakati pa anthu osakhulupirira. Muonetsetse kuti mu umboni wanu simukutsindika pa machimo ena kuposa ena, kupewa kuyamikira moyo wa uchimo.
2. Fotokozani za malo ndi nthawi yomwe inu munamva za Yesu, ndi chifukwa chimene chinakupangitsani kumulandira lye monga Mpulumutsi wanu. Pamene mukufokoza za kukhudzika mtima komwe kunadza pa inu, pempherani kuti Mzimu Woyera agwirensa ntchito yomweyo m’moyo wa munthu wina amene inu mukuchitira umboni wa Khristu kwa iye, kuti Mzimu abweretse mwa munthuyo mtima wolapa ndi womva chisoni chifukwa cha machimo ake.



NJIRA YOLALIKIRA UTHENGA WABWINO POGWIRITSA NTCHITO ZALA ZISANU

Njira iyi yolalikira uthenga wabwino yapafupi sisoweka zipangizo zapadera kapena mabuku. Nzeru ya chipulumutso ikufotokozedwa pogwiritsa ntchito zala za dzanja limodzi la munthu. Mu njirayi inu mumasoweka kuloweza mavesi pantima, koma ndi njira yotheka komanso yothandiza kwambiri popeza nthawi zonse inu mudzakhala wokonzeka kugawana uthenga wabwino ndi ena. Ngati womvera uthengayo akuoneka kuti ndi wokonzeka kukumvetserani, komanso ngati inu mukuona kuti ndi koyenera kutero, inutu mukhoza kugwira dzanja lake ndi kulozera ku chala chilichonse pachoka pamene mukumfotokozera iye tanthauzo la chalacho pogwiritsa ntchito vesi loloweza pantimalo.

1

Chala choyamba-Mulungu amakukondani

(Yohane 3:16).

“Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira lye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.”

2

Chala Chachiwiri - Onse anachimwa *(Aroma 3:23).*

“Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemmerero wa Mulungu.”

3

Chala Chachitatu-Khristu anafa kulipira machimo anu *(1 Akorinto 15: 3- 4)*

“Khristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu, monga mwa malembo.”

4

Chala Chachinayi- Khulupirirani kuti Khristu anafera machimo anu *(Yohane 1:12).*

“Koma onse amene amulandira lye, kwa iwo anapatsa mphamvu ya kukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake.”

5

Chala Chachisanu-Ngati mukhulupirira mudzalandira moyo wosatha *(Aroma 6:23).*

“Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.”



Mulimbikitse amene mukumulalikirayo kuchita chisankho ndipo kumpempherere kuti apeze chipulumutso.

Polemba



NJIRA YA CHIROMA YOPITA KU CHIPULUMUTSO

Njira yopita ku chipulumutso ikhoza kufotokozedwa pogwiritsa ntchito mavesi a m’Baibulo. Njirayitu ikuyenera kutsatidwa mwa ndondomeko yake, ndipo chidzakhala chinthu chothandiza kulemba mavesi onse amene inu mukuchita nawo m’Baibulo lanu. Ubwino waukulu wa njira yochitira umboni imeneyi ndi woti mavesi onse amakhala m’buku limodzi, zomwe zimapangitsa kuti kukhale kofewa ndi kwapafupi kwa inu kuwapeza. Mutamaliza kufotokozera mfundo yachinayi, onetsetsani kuti mukumaliza ndi kufunsa munthu amene mukulankhulana nayeyo ngati iye angafune kupemphera nanu pamodzi kuti alandire Khristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi wake.

1

Chosowa cha munthu (Aroma 3:23).

Onse anachimwa ndipo akusoweka chikhululukiro.

“Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemmero wa Mulungu.”

2

Mphotho ya uchimo (Aroma 6: 23).

Mphotho yake ya uchimo ndi imfa.

“Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa, koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.”

3

Chikonzero cha Mulungu (Aroma 5:8).

Mulungu anapereka njira yoperekera dipo la tchimo kupyolera mu imfa ya Yesu.

“Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha mmenemo, kuti pokhala ife chikhaliro ochimwa, Khristu adatifera ife.”

4

5. Yankho la munthu (Aroma 10:9).

Vomerezani machimo anu, Khulupirirani mwa Khristu, ndi kulandira chikhululukiro.

“Ngati udzavomereza ndi mkamwa mwako kuti Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka.”

NtchitoYoti Muchite

Ikani chizindikiro pa mavesi anayiwa m’Baibulo lanu ndi kuwaloweza pantima.



BUKU LOPANDA MAWU

Inu mukhoza kuuza wina aliyense uthenga wa chipulumutso pogwiritsa ntchito Baibulo lanu ndi kabuku kakang'ono kodabwitsaka! Mulole kukambirana ndi munthuyo. Muyenera kumawerenga ndemanga zokhudza Mawu a Mulungu. Pamene mukuchitira umboni ndi koyenera kuti inu mugwiritse ntchito mavesi ochepa. Muyambe zokambirana zanu ndi munthuyo pomuza dzina lanu komanso kumufunsa dzina lake, kuti muzitha kumutchula dzina mu zokambirana zanu zonse. Onetsetsani kuti mukufotokoza nkhani yanu mopatsa chidwi ndi mwamphamvu. Iyi ndi njira yomwe ingathandize kuti amene mukulankhula nayeyo apeze chipulumutso!

Kufotokoza Nthano

Kodi munayamba mwaonapo buku lopanda mawu kapena zithunzi? (Wayulani m'mwamba masamba a buku kuonetsa mtundu wake.) Buku ili limene masamba ake ndi a mitundu yosiyanasiyana muli nthano yopatsa chidwi kwambiri yochokera m'Baibulo yokamba za Mulungu woona ndi wamoyo amene analenga dziko lapansi. Ine ndalitchula buku langali kuti 'Buku Lopanda Mawu'. Mtundu wa tsamba lililonse la bukuli likundikumbutsa gawo lina la nthanoyi. Kodi inu mungafune mutaimva? (Dikirani yankho kuchokera kwa munthuyo.)



Pitani ku Tsamba la Golidi

(Zomwe tikudziwa zikusonyeza kuti ndi chinthu chanzeru kuyambira pa tsamba la golidi, kutsindika za chikondi cha Mulungu.)

Tsamba la golidi limandikumbutsa kumwamba. Kodi inu mukudziwa kuti kumwamba ndi chiyani? (Dikirani yankho kuchokera kwa munthuyo.) Kumwamba ndiko kwawo kwa Mulungu. Baibulo limatiuza kuti misewu ya mzinda wa kumwamba, ndi ya golidi woyengeka, wofanana ndi mandala openyekera (*Chivumbulutso 21:21*). Mulungu amatiuza zambiri zokhudza kwawoko. Kumeneko kulibe kudwala konse. Kulibe konse imfa. ulibe konse usiku. Kumwambako aliyense adzakhala wokondwa koposa (*Chivumbulutso 21:4-23*). Chodabwitsa kwambiri kumwambako ndi choti kuli Mulungu Atate ndi Mwana Wake, Ambuye Yesu Khristu.

Mulunguyo ndi amene analenga zonse. Analenga inunso, ndipo amakukondani kwambiri. “Baibulo likuti, “Pakuti Mulungu adakonda dziko lapansi. . .”(Yohane 3:16). Izi zikutanthauza kuti Mulungu amakonda aliyense kuphatikizapo inu ndi ine. Popeza Mulungu anakulengani ndipo amakukondani, Iye akufuna inu mukhale gawo la banja Lake komanso kuti mudzakhale ndi Iye tsiku lina (Yohane 14:2). Kumwamba ndi malo apamwambatu nanga. Kumwamba ndi kwangwiro chifukwa Mulungu ndi wangwiro. Koma pali chinthu chimodzi chimene sichidzapezeka konse kumwambako.



Mupite ku Tsamba Lakuda

Muwiritse ntchito tsamba limeneli pofuna kutsindika za chosowa chاوزimu cha womverayo. Pamene mukunena za tchimo, pempherani kuti Mzimu Woyera adzakhudze munthuyo.)

Chinthu chimodzi chimene sichidzakhala konse kumwambako ndi tchimo. Tsamba lakudali likundikumbutsa za tchimo. Chifukwa choti inu ndi ine ndi ochimwa tikufuna kuchita zinthu mu njira ya ife eni mmalo motsata njira ya Mulungu. Tchimo ndilo kufuna kuchita zinthu mu njira ya ife eni. Kuchita, kapena, kunena, kapena kuganiza zinthu zoipa ndi tchimo. Tchimo ndilo kusamvera malamulo amene Mulungu wapereka m’buku Lake, Baibulo. Tchimo limadzetsa chisoni m’dziko lapansi. Kodi mungaganize zinthu zina zimene ndi tchimo? (Dikirani yankho.) Kodi mukudziwa kuti ndinu wochimwa? Mawu a Mulungu akuti, “Pakuti onse anachimwa” (Aroma 3:23). Mawu oti onse akutanthauza tonsefe. Tchimo limachotsa inu ndi ine kwa Mulungu chifukwa Iye ndi wangwiro, ndi wopanda tchimo konse. Mulungu sangalole kuti tchimo likhale kumene Iye aliko.

Mulungu akuti wochimwa ayenera kulandira chilango. Chilango cha uchimo ndiyo imfa, kulekanitsidwa ndi Mulungu kwamuyaya (**Aroma 6:23**). Mulungu anadziwa kuti palibe chomwe inu mukadachita kuti muchotse tchimo lanu. Iye anadziwa kuti inu simukadakhala wabwino woti nkumukondweretsa Iye. Koma Iye amakukondani ndipo akufuna mukhale mwana Wake. Chotero, Iye anapanga njira yoti inu mukhululukidwe.



Pitani ku tsamba lofiira

(Gwiritsani ntchito tsamba limeneli potsindika za njira ya chipulumutso kupyolera mu imfa ya Khristu.)

Tsamba lofiira limasonyeza njira ya chipulumutso. Mulungu amakukondani kwambiri. Iye anatumiza Mwana Wake wobadwa yekha, Ambuye Yesu Khristu ku dziko lino lapansi kuchokera kumwamba. Iye anabadwa ngati mwana wakhanda kenaka nakula kukhala munthu wamkulu. Yesu anali wosiyana ndi munthu wina aliyense amene anakhalapo padziko lino lapansi. Iye sanachite cholakwa ngakhale chimodzi. Iye ndi wangwiwo.

Koma tsiku lina anthu ochimwa anamuveka chisoti cha minga pamutu Pake namupachika pamtanda. Baibulo likuti Khristu ali pamtandapo, Mulungu anaika machimo athu onse pa Iye (*Yesaya 53:6*). Mkwiyu wanu wonse, mabodza ndi kumana kwanu konse, machimo anu onse, zonse zinaikidwa pa Mwana wa Mulungu.

Kodi pamene Yesu anakhomedwa pamtanda ndi chiyani chomwe chinatuluka kuchokera m'manja ndi m'mapazi Mwake? (Mwazi.) Baibulo limati popanda kupereka mwazi, palibe chikhululukiro (*Ahebri 9:22*). Yesu anatenga chilango chanu cha imfa chifukwa cha tchimo lanu. Iye anasautsidwa kwambiri. Ndipo kenaka Iye anafuula ndi mfuu waukulu, nati "Kwatha." Ambuye Yesu anadza ku dziko lino lapansi kudzatenga chilango chathu chodza kamba ka tchimo lathu. Ndipo Iye anatsiriza ntchitoyi pofa pamtanda. Baibulo likuti, "Khristu anafera zoipa zathu. . .ndi kuti anaikidwa" m'manda (*1 Akorinto 15:3, 4*). Koma patapita masiku atatu chinthu chodabwitsa kwambiri chinachitika; Mulungu anamupatsanso moyo. Mulungu anaukitsa Yesu kwa akufa. Yesu ndi Mpulumutsi wamoyo (*1 Akorinto 15:4*). Iye akufuna kukhala Mpulumutsi wanu, kuti akupulumutseni ku machimo anu.

(Mufunseni munthuyo kuti achite chisankho ndi kumupempha kupemphera nanu kuti alandire Khristu.)



Pitani ku tsamba loyera

(Mugwiritse ntchito tsamba limeneli kutsindikira zokhudza mbali ya womverayo, kuti akhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu monga Mpulumutsi wa moyo wake.)

Tsamba loyerali likundikumbutsa kuti mukhoza kuyeretsedwa ku machimo anu (*Masalimo 51:7*). Mulungu akutiiza izi m'Baibulo. Muuzeni munthuyo kuti awerenge nanu vesi lonseli.) "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti adapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha" (*Yohane 3:16*). Inde, Mulungu

amakukondani. Mulungu akuti ngati inu mukhulupirira mwa Yesu Khristu simudzatayika, inu simudzalekanitsidwa ndi Mulungu kwamuyaya. Iye adzakukhululukirani machimo anu ndi kukupangani kukhala woyera pamaso pa Mulungu. Mulungu akuti, “yense wakukhulupirira.” Mukhoza kuika dzina lanu mmalo mwa mawu oti “yense.” Ngati inu mukhulupirira pa Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wanu; Iye adzakupatsani moyo wosatha kumwamba. Ngati mukhulupirira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wanu, Iye adzakukhululukira tchimo lanu. Ndipo Iye adzakhala ndi inu nthawi zonse ndi kukupatsani mphamvu zokuthandizani kumvera Mulungu. Inu lero mukhoza kumuza Yesu kuti mwachimwa, ndi kuti mukukhulupiriranso kuti Iye anafera inu. Baibulo likuti, ngati mulapa (zomwe zikutanthauza kusiya) tchimo lanu, tchimolo lidzafafanizidwa (*Machitidwe 3:19*). Baibulo likunenanso kuti ngati inu mukhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu mudzapulumuka (*Machitidwe 16:31*). Kodi inu mungakonde kuchita motero ndi ine tsopanoli? (Ngati yankho ndi inde, inu mupemphere naye munthuyo kuti alandire Khristu monga Mpulumutsi wake.)



Pitani ku tsamba lobiriwira

(Pa tsamba limeneli mutsindike za kukula kwa uzimu.)

Mtundu wobiriwira umandikumbutsa za zomera zimene zimakula, monga masamba, udzu, maluwa ndi mitengo. Tsamba limeneli limandikumbutsa za moyo watsopano, moyo wosatha, umene inu mwalandira kuchokera kwa Mulungu. Ngati mukhulupirira mwa Yesu Khristu monga Mpulumutsi wokupulumutsani ku tchimo, inu mumakhala ngati mwana amene wangobadwa kumene m’banja la Mulungu. Mulungu akufuna kuti inu mukule mu njira yapadera. Baibulo likukuuzani kuti “koma kulani . . . m’chizindikiritso cha Ambuye wathu ndi mpulumutsi Yesu Khristu” (*2 Petro 3:18*).

Pamene mukuphunzira za Yesu kuchokera m’Baibulo inu mudzaphunzira mmene mungapewere tchimo (*Masalimo 119:11*). Tsiku ndi tsiku mfunseni Iye kuti akuthandizeni kumumvera. Mukachimwa muuzeni Mulungu kuti mwachimwa. Iye akukhululukirani nthawi yomweyo. Baibulo likuti, “Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse (*1Yohane 1:9*).

Mpempheni Mulungu akuthandizeni kuti musadzachitenso cholakwacho.

(Mutsogolereni munthuyo kuthokoza Mulungu chifukwa cha lonjezo Lake loti akuthandizani.)

1. Lankhulani kwa Mulungu-Pempherani (1 Atesalonika 5:17). Baibulo likutiiza kuti tipemphere kosaleka.
2. Mvetserani kwa Mulungu-Phunzirani Mawu a Mulungu powerenga ndi kuwaloweza pamtima (*Masalimo 119:11*).
3. Lankhulani kwa ena mmalo mwa Mulungu-chitirani umboni kapena uzani ena -za lye (Marko 16:15).
4. Mupembedzeni-muzipita ku Sunday sukulu, kutchalitchi, ndi ku magulu ang'ono ang'ono (*Ahebri 10:25*).

Munthuyo asanachoke,

1. Mumupatse thirakiti kapena maphunziro owerega ndi kuphunzira kunyumba.
2. Muuzeni apemphere “pemphero lothokoza” chifukwa cha zimene Ambuye Yesu Khristu wamuchitira.
3. Pempherani limodzi ndi wokhulupirira watsopanoyo, kenaka mumuuze kuti apemphere payekha.
4. Mumupemphe kuti akupatseni dzina ndi adiresi yake kuti muzitha kumutsatira.

[Malangizo a Buku Lopanda Mawu ndi thandizo lochokera ku gulu la Child Evangelism Fellowship.]

Munthuyo asanachoke,

1. Kodi ndi iti ya njira zofalitsira Uthenga Wabwino yomwe ili yopambana ndi yothandiza kwambiri kwa inu kugwiritsa ntchito, nanga ndi chifukwa chiyani?
2. Kodi ndi malo ena ati ndi nthawi zina ziti kumene ndi zimene mungagwiritse ntchito buku ili Lopanda Mawu pochitira umboni?

Vesi Lotsogolera: Aroma 1:16a

*“Pakuti uthenga wabwino sundichititsa manyazi;
 pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa
 munthu aliyense wakukhulupirira; kuyambira
 Myuda, ndiponso Mhelene.”*



Malembo okhudza mkazi wa ku Samariya: Yohane 4:4-42

Mawu Oyamba

1. Yesu anakakamizidwa ndi Mzimu Woyera kudutsa mu Samariya kukagwira ntchito ya umulungu.

2. Apaulendo a Chiyuda kawirikawiri anali kuyenda mozungulira Samariya, ulendo wa masiku asanu ndi limodzi, pofuna kupewa kukhudzana ndi Asamariya, amene Ayuda ankaganiza kuti anali anthu otsikirapo poyerekeza ndi iwo eni chifukwa Asamariya sanali

Ayuda enieni,
 popeza iwo anali kukwatirana ndi anthu amitundu.



3. Yesu ndi ophunzira Ake

akupita ku Samariya kukachita mkumano muwosintha moyo ndi mkazi mmodzi yekha.

Makhalidwe a munthu wopindula miyoyo amene tingaphunzire kuchokera kwa mkazi wa ku Samariya wa ku Samariya

1. Wopindula miyoyo ndi wochimwa chabe amene wapeza chipulumutso mwa Khristu (Machitidwe 4:12)

a. Mkazi wa ku Samariyayu akuimira tonsefe, ngakhale kuti Malembo sakumutchula dzina.

b. Iye anakumana ndi zotchinga zingapo:

- **Zotchinga zokhudza kusankhana malingana ndi mtundu wa khungu\ chikhalidwe**-anali Msamariya
- **Zotchinga zokhudza chomwe ankachita m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku**- anali mkazi wadama, woyenda ndi amuna a eni (Yohane 4:18)
- **Zotchinga zokhudza chipembedzo**- Iye anali wa gulu la anthu (Asamariya) amene mapembedzedwe awo anali osiyana ndi Ayuda (Yohane 4:21-23).
- Yesu sanalabadire za zotchinga zonsezi pamene anakalankhula ndi mkazi ameneyu (Yohane 4:7)

c. Mkaziyu anakumana ndi mavuto akulu okhudza khalidwe (Yohane 4:16-18).

- Iye anali kapolo wa tchimo womvetsa chisoni.
- Maubale ake analephera kukwaniritsa zokhumba za mtima wake (Masalimo 38:4).

d. Kukumana kamodzi ndi Yesu Khristu kunasintha moyo wake kwamuyaya.

- Yesu anayankha mafunso ake onse modekha (Yohane 4:12-26).
- Yesu anamutengera ku choonadi (Yohane 4:24).
- Yesu anakwaniritsa chosowa chake chofuna kupeza Mpulumutsi (Yohane 4:26).

e. Yesu anadza kudzampatsa mkaziyu chinthu chimodzi chimene iye ankachisowa koposa zonse: chipulumutso-moyo watsopano! Mu njira yomwe Yesu anafikira kwa mkazi wa ku Samariyayu, Iye anali chitsanzo cha wopindula miyoyo wopambana.

- Yesu anasintha moyo wake- mkaziyu anagonjetsa zotchinga zonse, polalikira kwa aliyense amene amkatenga iye ngati munthu wotsalidwa (Yohane 4:28-29).
- Yesu anasintha cholinga cha mkaziyu –tsopano cholinga chake chachikulu chinakhala kuchitira umboni Khristu (Yohane 4:39).
- Yesu anasintha zinthu zonse –anthu onse a m’udzi momwe mkaziyu ankakhala anakhala okhulupirira a Yesu (Yohane 4:42).
- Pamapeto pake Yesu akupereka kwa okhulupirira kupezeka Kwake (Mlaliki 33:14; Mateyu 1:23), ndipo izi zikuwapanga iwo kukhala opindula miyoyo.

2. Wopindula miyoyo ndi munthu amene wakhutitsidwa mwa Yesu Madzi Amoyo (Yohane 4:10 – 15).

- a. Okhulupirira amapeza chokhutitsidwa nacho mwa Yesu chifukwa lye mwini ndi mphatso ya Mulungu imene yapatsidwa kwa iwo, kuwapulumutsa ku imfa yamuyaya (Yohane 4:10, onaninso Yohane 4:16; 2 Akorinto 9:15). Amene ali wokhutitsidwa mwa Yesu amafunitsitsa atagawana nkhani yabwinoyi ndi ena (Yohane 4:28-29).
- b. Madzi ndi chinthu chofunikira kwambiri ku moyo wa munthu. Gawo loposa 70 percent ya thupi la munthu komanso dziko lapansi ndi lodzazidwa ndi madzi. Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha madzi a pachitsime pofuna kufotokoza kukhutitsidwa komwe wokhulupirira amapeza mwa lye kupyolera mu chipulumutso chimene amapereka. Yesu amabweretsa kukhutitsidwa kodzaza chifukwa lye ndi:
 - Madzi Amoyo (Yohane 4:10). Yesu amapereka moyo wosatha (Yohane 4:4).
 - Madzi wothetsa ludzu (Yohane 4:13). Ludzu lathu lauzimu limathetsedwa ndi Yesu Khristu yekha basi: Munthu amene adza kwa iye sadzamva njala yauzimu konse; ndipo iye amene akhulupirira mwa lye sadzamva ludzu lauzimu (Yohane 6:35).
 - Madzi woyeretsa-wosintha moyo (Yohane 4:16-19). Kukumana kwa mkazi wa ku Samariya ndi Yesu kunamusintheratu, kumuyeretsa, kuchotseratu tchimo lake.

Kusinthaku kukhoza kuoneka chifukwa, ngakhale iye sanali wolandiridwa ndi anthu, (pobwera kudzatunga madzi ku chitsime pa nthawi yomwe anthu ambiri sapita kuchitsimeko) iye anapita kukagawana ndi mudzi wonse nkhani ya Khristu (Yohane 4:28-29). Ngakhalenso lero, mwazi wa Yesu umatiyeretsa kutichotsera machimo athu onse ndi kutipanga kukhala cholengedwa chatsopano (2 Akorinto 5:17).

- **Madzi wotumphukira (Yohane 4:14).** Madzi (kutha kwa ludzu) womwe Yesu amapereka amasanduka kasupe wa madzi wotumphukira ku moyo wosatha mwa wokhulupirira (Yohane 7:37-39). Pamene wokhulupirira walandira Mzimu Woyera, Yesu amakhala gwero lake lopereka moyo mwa iye nthawi zonse.

c. Monga mmene zinalili ndi mkazi wa ku Samariyayo, moyo wa wopindula miyoyo uyenera kuonetsera kuti iye mwini anamwa madzi a moyo (kuti iye ali ndi chipulumutso mwa Yesu Khristu.) Kutumphukira kwa madziku kuyenera kutumphukira kwa aliyense ndi kumpangitsa kufikira anthu ena ochuluka ndi uthenga wabwino.

3. Wopindula Miyoyo ndi munthu amene ali ndi uthenga (Yohane 4:29).

Wopindula miyoyo pokhala wopulumutsidwa ndi Yesu komanso wokhutitsidwa mwa lye nthawi zonse, iye amakhala ndi uthenga woti agawane ndi ena monga mmene anachitira mkazi wa Samariyayu.

- a. Uthenga wa **Choonadi**: “Tiyeni mukaone munthu, amene anandiuza zinthu zilizonse ndinazichita (Yohane 4:29). Iye ankadziwa bwino lomwe kuti zimene Yesu anamuuzazo zinali choonadi. Ife tili ndi uthenga wa Yesu amene ndi Choonadi (Yohane 4: 6).
- b. Uthenga wa **Chiyembekezo**: “. . . ameneyu sali Khristu nanga?(Yohane 4:29). Mkaziyu anali ndi uthenga wabwino woti Mesiya akubwera ku mudzi kwawo. Kunena zoonza, Asamariyawo, anthu omwe anali pansu pa mdima wauzimu, komanso chilamulo ndi malamulo ena, anali kudikira Mesiya mwachidwi. Mkaziyu anawabweretsa uthenga wa chiyembekezo: lyetu akhoza kukhala Mesiya,

ndithudi ndi Iye amene (Yohane 4:26)!

c. Uthenga wobetchera: “ameneyu sali Khristu nanga?” (Yohane 4:29). Mkaziyu anatakasa chidwi chawo kuti iwo aganize ndi kuchitapo kanthu.

d. Uthenga Wowaitanira kwa Khristu: “Tiyeni mukaone munthu. . .” (Yohane 4:29). Ndi uthenga wake wa choonadi, chiyembekezo, ndi wobetchera, mkaziyo anaitana anthuwo kuti abwere kudzakumana ndi Yesu maso ndi maso.

4. Wopindula Miyoyo amakhala mboni ya Yesu ya chidwi

(Yohane 4:28). Iye amakhala:

a. **Wachimwemwe** (Yohane 4:28). Mkazi wa ku Samariyayu anali ndi chimwemwe chachikulu, nasiya mtsuko wake wa madzi kumbuyo. Iye analandira Madzi Amoyo, (Yesu), ndipo anayeretsedwa, kukwanitsidwa, ndi kusefukira ndi chimwemwe cha cholowa chosatha.

b. **Wolimba Mtima** (Yohane 4:28). Iye anabwerera ku mudzi wa kwawo, ngakhale mbiri yake inali yoipa kumeneko. Iye anapita kwa anthu omwewo amene ankamuona monga wosalidwa ndi wosalandirika pakati pawo.

c. **Wopanda Mantha** (Yohane 4:29). Mkaziyu anabetchera anthuwo kuti “Tiyeni mukaone.” Iye analalikira kuti Yesu akhoza kukhala Khristu ndi kupereka chidwi kwa iwo kuti apite kwa Yesu.

d. **Wopanda Manyazi** (Yohane 4:29). Iye anati, “anandiuza zinthu zilizonse ndinazichita.” Potero, iye anavomereza zinthu zonse zimene anzichitazo, zomwe zikanakhala zochititsa manyazi kwa iye kovomereza nthawi ya kumbuyo Yesu asanamuyeretse. Iye sanachite manyazi kufotokoza umboni wa kusinthidwa kwake.

e. **Iye anali wachidwi** (Yohane 4:29). Nthawi yomweyo iye anachitira umboni za Yesu. Iye sanataye nthawi ndi kufunsa munthu wina zoti achite ndipo sanachite mantha ndi zomwe zikanamugwera chifukwa cha kulimba mtima kwakeko. Iye anachita izi mwachangu, popeza Yesu anali pa ulendo wopita ku mudzi wina.


f. Wobala Chipatso (Yohane 4:39-42). Umboni wa mkaziyu unapangitsa Asamariya ambiri a m'mudzi mwakemo kukhulupirira Yesu ndi kudza kwa Iye. Yesu mwini anawaphunzitsa yekha kwa kanthawi kochepe, kuti aliyense wa iwo amu khulupirire monga munthu payekha. Iwo sanakhulupirira mwa mkaziyu, koma mwa Khristu mwiniitchitu ndi chizindikiro chimodzi cha mboni yabwino-iye akupangitsa anthuwo, aliyense payekha kukhala mu chikhulupiriro chopulumutsa mwa Yesu Khristu.

Mafunso Okambirana:

1. Mkazi wa ku Samariya anakumana ndi chiweruzo kuchokera kwa anthu a m'mudzi wa kwawo chifukwa cha khalidwe lake lochimwa. Yesu anagonjetsa chotchinga chimenechi nachitira umboni kwa iye. Kodi inu mungagonjetse bwanji zotchinga zobwera kamba ka chikhaliidwe mu kuyesetsa kwanu kofuna kulalikirira uthenga wabwino?
2. Tchulani makhalidwe asanu ndi limodzi a munthu wa chidwi chofuna kuchitira umboni monga anachita mkazi wa ku Samariyayu? Kodi ndinu mboni ya chidwi? Chifukwa chiyani zili chomwecho, ngati si choncho, nanga ndi chifukwa chiyani?

Pemphero

Ambuye mundipange kukhala wopindula miyoyo wobala chipatso. Thandizeni kukhala wa chimwemwe, wolimba mtima, ndi wopanda mantha kuuza aliyense amene ndikumudziwa za Yesu, amene ndi Madzi Amoyo. Kenaka mundithandize kukhala wophunzitsa ndi kupanga anthu ena kukhala ophunzira a Yesu ndipo muthandize anthu amene ndikuphunzitsawo kukula kufikira atabala chipatso. Amen.



Vesi Lotsogolera: Tito 2:3-4a

“Momwemonso akazi okalamba akhale nawo makhalidwe oyenera anthu oyera, osadierekeza, osakondwa nacho chikondi cha pa vinyo, akuphunzitsa zokoma; kuti akalangize akazi ang'ono akonde amuna awo, akonde ana awo.”



Malembo: Buku la Rute

Mawu Oyamba

1. Mfundo yoti ophunzira a Yesu aitsatire pa udindo wawo inaperekedwa ndi Yesu mwini. Yesu anasankha ophunzira khumi ndi awiri, ndipo kenaka iye anasankha atatu a iwo kukhala oyandikana naye kwambiri (Petro, Yakobo ndi Yohane), kuwaphunzitsa mowirikiza. Iwo anakhala limodzi kwa nthawi yochepa, komabe iyi inali nthawi yabwino ndithu.
2. Cholinga cha wopanga ena kukhala ophunzira a Khristu ndi kulimbikitsa kukula kwa anthu amene ali ndi kuthekera kokhala atsogolero ndi kuwapatsa zowayenerenza mu utumiki (2 Timoteo 4:1-2). Dzina lina la munthu wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ndi mulangizi (mpangiri), amene wafotokozedwa monga “mphunzitsi wanzeru kapena wokhulupiriridwa kapena wopereka uphungu.” Munthu amene akuphunzitsidwa ndi mulangiziyo amatchedwa “wolangizidwa.”
3. Chitsanzo cha mfundo imeneyi tingachipeze m'buku la Rute (wolangizidwayo), ndi kuphunzira ubale wake ndi Naomi (mulangizi wakeyo).

Makhalidwe a Mulangizi Wabwino

1. Mulangizi wabwino **salabadira zotchinga zokhudza chikhalidwe kapena mtundu wa munthu (Rute 1:3-4)**. Naomi anali Myuda pamene Rute anali M'moabu.
 - a. Zotchinga zokhudza mtundu wa khungu la munthu, ntchito imene amagwira, ndi chikhalidwe chake, zimakhala gawo la dziko lapansi, koma izi sizikuyenera kukhala gawo la ufumu wa Mulungu.
 - b. Lamulo la ufumu wa Mulungu ndi chikondi. Chikondi chitikakamiza kufikira ngakhale anthu amene ndi osiyana ndi ife.
 - c. Pamene tikufuna munthu woti timupatse upangiri kapena uphungu, ife tiyenera kukhala ndi maso a Mulungu, amene saona zotchinga zokhudza chikhalidwe kapena mtundu wa khungu la munthu (2 Petro 3:9).
2. Alangizi abwino **amakhala ndi masomphenya/ cholinga (Rute 1:6-7)**. Naomi anadziwa kumene anali kupita- anali kubwerera ku Yuda.
 - a. Alangizi ayenera kudziwa kumene akupita. Kodi chotsatira chomaliza cha ubalewo ndi chiyani? (Miyambo 29:29:18).
 - b. Kuphunzitsa munthu kukhala wophunzira wa Yesu ndi koposa kupititsa mtsogolo kuthekera kwa munthu mwini; uku ndi kuphunzitsa wina kukhala monga Khristu mwini (2 Akorinto 3:18).
3. Alangizi abwino **amamulola munthu amene akumulangizayo kusankha chimene iye akufuna kukhala ndi kuchita (Rute 1:8-9)**. Naomi analola Olipa ndi Rute kusankha chimene iwo akadafuna kuchita.
 - a. Mulungu anapatsa anthu ufulu wosankha zimene adzachite (Deuteronomo 30:19).
 - b. Si udindo wa mulangizi kusankhira ndi kukakamiza munthu amene akumupatsa upangiriyo zoti achite.
 - c. Mulangizi wabwino amafotokoza njira yoti mkutsatiridwayo momveka bwino ndi kulola wolangizidwayo kukhala ndi mpata wosankha kutsata njirayo kapena kuikana.

d. Alangizi ayenera kukhala olimbikitsa ndi okonda munthu amene akumulangizayo, ngakhale pamene wolangizidwayo walakwitsa.

4. Alangizi abwino **amayang'anira ndi kuyendetsa zinthu mwaumulungu (Rute 2:19)**. Naomi analimbikitsa Rute kuchita zinthu mosamalitsa.

a. Alangizi abwino amakhala akulumikizani ndi kudzudzula wolangizidwayo nthawi ndi nthawi pa zinthu zimene iye wachita mopanda nzeru.

b. Cholinga cha kuchita zinthu mosamalitsa si kulamulira, koma kuphunzitsa ndi kulangiza wolangizidwayo.

5. Alangizi abwino **amapereka chidziwitso ndi nzeru zawo kwa amene akulangizidwawo (Rute 2:20)**. Naomi ankadziwa chikhaliidwe ndi machitidwe a Ayuda- Rute sankadziwa zimenezi. Naomi anaphunzitsa Rute zinthu zimenezi ndi kumulangiza kutsatira ndondomeko yoyenerera.

a. Alangizi ayenera kuonjezera nzeru ndi luso lawo kuthandiza munthu amene akumulangizayo kusintha mwanzero m'moyo wake wotsatira.

b. Nzeru zimadza podziwa Mawu a Mulungu ndi kukhala ndi nthawi yolankhula kwa Mulungu amene adzapereka chidziwitso mu gawo lililonse la moyo wa munthu komanso mu gawo lililonse la utumiki.

c. Cholinga cha alangizi abwino chimakhala chomupanga wolangizidwayo kuti pamapeto pake adzakhale wodalira pa nzeru za Mulungu, osati za iye mwini.

6. Alangizi abwino **amapereka uphungu wa umulungu (Rute 22,3:3-4)**. Naomi anagwiritsa ntchito nzeru zake kupereka malangizo abwino kwa Rute.

a. Malangizo a umulungu amachokera m'Mawu a Mulungu. Mu kuphunzitsa munthu kukhala wophunzira wa Yesu, malangizo sayenera kuperekedwa molingana ndi nzeru za munthu kapena zimene iye akuona (Miyambo 2:6).

b. Uphungu sumangokhudza kufotokoza chabe, (Yakobo 1:19).

c. Moyo wa umulungu wa mulangizoyo umathandiza wolangizidwayo kumvera ulamuliro wake.

7. Alangizi **abwino amakhala ndi mitima yosamala (Rute 3:1)**. Naomi anali wokhudzika ndi umoyo wa Rute.

a. Alangizi ayenera kukumbukira kuti iwo ndi akazembe komanso njira yodzera chikondi cha Mulungu kupita kwa anthu amene akuwalangizawo.

b. Chifundo ndi chikondi, pamodzi ndi malangizo odzudzula tchimo mopanda mantha, zidzapangitsa kuti zonse ziyende bwino (Aefeso 4:32).

Khalidwe la Wolangizidwa Wabwino

1. Olangizidwa abwino **amakhala odzipereka ndi omvera alangizi awo (Rute 1:14-17)**. Rute anali wodzipereka ndi womvera kwa Naomi, kusonyeza chikondi, kukhudzika ndi ulemu.

a. Iye anali wokonzeka kusiya chipembedzo chake chimene anakhala akupembedza moyo wake wonse ndi kudzipereka kuyamba kupembedza Mulungu wa Naomi (Miyambo 28:13; Machitidwe 3:19).

b. Chikondi cha Rute chinaonetseredwa mu khumbo lake lokana kubwerera ku nyumba ya mayi wake, nasankha kukhala ndi Naomi (1 Petro 1:22).

2. Olangizidwa abwino **amakhala omvera (Rute 3:5)**. Rute atapatsidwa langizo ndi Naomi, iye anachita ndendende zimene analangizidwa kuchitazo.

a. Mtima womvera umakhalanso mtima wodzichepetsa ndipo ili ndi khalidwe lofunikira kwambiri m'maubale opanga anthu ena kukhala ophunzira a Yesu (Masalimo 51:10-12).

b. Iwo amene akudza kwa Mulungu ayenera kudza ndi mitima yawo yomwe osati maganizo awo okha (Yohane 4:24).

2. Olangizidwa abwino amakhala nawo maganizo a iwo eni (Rute 2:2). Rute anapempha yekha kwa Naomi kupita kukakunkha tirigu kuminda.

a. Olangizidwa ayenera kuganiza mwakuya ndi kukhala ndi maganizo atsopano, ngakhale zimene iwo sanaziyeserepo kuchita chiyambire (Yesaya 43:19).

b. Kuyesera kuchita chinthu china chatsopano, ngakhale chitamaoneka ngati chosatheka, ndi njira imodzi imene ophunzira a Yesu amaphunzira ndi kukula nacho.

4. Olangizidwa amafotokoza zochitika mokhulupirika ndi momveka bwino (Rute 2: 19-22).

a. Rute anayankha mafunso a Naomi mopanda mantha.

b. Iye anayankha mokhulupirika ndi momveka bwino, kumuza Naomiyo zonse zimene iye akadazisowa kuti zimuthandize kupereka upangiri wabwino (1 Petro 3:15).

Madalitso a Ubale Wolangiza

1. Alangizi ndi olangizidwa, onse amagawana madalitso a Mulungu (Rute 3:16-18; 4:14-16). Naoni anagawana nawo mdalitso wa Rute.

a. Cholinga chachikulu cha ubale wa pakati pa olangiza ndi olangizidwa ndi choti onse apeze Ufumu wa Mulungu, ndi kulandira mdalitso pamodzi.

b. Olangiza akuyenera kukondwera ndi chipambano cha olangizidwa, ndipo iwo sayenera kuchita nsanje chifukwa cha chipambano chotero (1 Petro 2:1).

c. Madalitsowo ayenera kukhala opatsirana ndi opitirira, pamene wolangizidwayo akutenga udindo wa wolangizayo kukhala wake ndi kuopitiriza pa ena.

2. Olangiza ndi olangizidwawo pamodzi amabweretsa madalitso kwa ena komanso ku ufumu wa Mulungu (Rute 4:18-22). Kupyolera mu ubale wa Naomi ndi Rute, ndipo kenaka kukwatirana kwa Rute ndi Boazi, banja latsopano linakhazikitsidwa ndi kubweretsera mdalitso ndi chimwemwe chachikulu kwa iwo.

Pamene anthu a Mulungu akugwira ntchito limodzi mogwirizana, ufumu Wake umadalitsika (Masalimo 133:1). Kupyolera mwa Yesu wa mbumba yochokera mwa Rute ndi Boazi, dziko lonse lapansi linadalitsika (1 Akorinto 15:22).

Mafunso Okambirana

1. Kodi makhalidwe ofunikira a mulangizi wabwino ndi ati? Nanga inu muli ndi makhalidwe otero? Kodi ndi khalidwe liti la makhalidwe amenewa limene lili lovuta kwambiri kulionetsera, nanga ndi chifukwa chiyani?

2. Kodi makhalidwe abwino a wolangizidwa wabwino ndi ati? Nanga inu muli nawo makhalidwe otero? Kodi ndi khalidwe liti lomwe lili lovuta kwambiri kulionetsera, nanga ndi chifukwa chiyani?

Pemphero

Ambuye Yesu, thandizeni kukhala mulangizi wabwino, woonetsera chifundo ndi chikondi komanso wogawana ndi ena nzeru zimene mwandipatsa. Chonde sonyezeni mmene ndingalangizire olangizidwa ndipo mundithandize kukhala wolangizidwa (mphunzi) wabwino ndi wokhulupirika kwa anthu amene akundiphunzitsa njira Zanu. Dziko lapansi lidalitsike kupyolera mu ubale wolangiza momwe ine ndingatenge mbali mu ntchito yabwino yopanga ena kukhala ophunzira anu. Amen.



10

*Priskila: Wopanga Ena
Kukhala Ophunzira a Yesu*

Vesi Lotsogolera: 2Timoteo 4:2

*“Lalikira mawu; chita nawo pa nthawi yake,
popanda nthawi yake; tsutsa, dzudzula, chenjeza,
ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitsa.”*



Malembo momwe Priskila watchulidwa: Machitidwe 18:1-4, 18-22, 24-26; Aroma 16:3-4; 1 Akorinto 16:19; 2 Timoteo 4:19

Mawu Oyamba

1. Akula Myuda wochokera ku fuko la Ponto, m'dziko la Italy anabwera mu Korinto nakhazikika mmenemo pamodzi ndi mkazi wake Priskila (Machitidwe 18:2). Iye anathamangitsidwa kwawo potsatira lamulo la Claudius mfumu yaikulu ya Roma m'chaka cha 52 A.D loti Myuda aliyense achoke mu Roma. Priskila ndi Akula atchulidwa kasanu ndi kamodzi (6) m'Chipangano Chatsopano. (Onani Malembo amene ali pamwambapa.)
2. Nthawi zonse zomwe iwo atchulidwa, iwo atchulidwa monga banja osati payekha-payekha.
3. M'malo anayi dzina la Priskila ndi lomwe latchulidwa koyamba. Uku ndi kuchuka kwachilendo kwa mkazi m'gulu la anthu mmene amuna ndi amene anali ndi ulamuliro waukulu.
4. Makhalidwe achisanu ndi limodzi (6) amene ali mu mndandanda wotsatirawu akuonetsera momwe utumiki wa Priskila ndi Akula ukutiphunzitsira ife kukhala olimbikira pa ntchito yopanga ena kukhala ophunzira a Yesu.

Makhalidwe Asanu ndi Limodzi a Munthu Wopanga Ena Kukhala Ophunzira a Yesu (monga mmene aonetseredwa m'moyo wa Priskila)

1. Wopanga ena kukhala wophunzira a Yesu ayenera kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kukhala wokonzeka kumvera Mawuwu nthawi zonse (Machitidwe 18:1-11, 26).
 - a. Ndi zoonekeratu kuti Priskila ndi Akula anali Akhristu odzipereka.
 - b. Mulungu mu chisamaliro Chake, anagwiritsa ntchito luso lawo losoka mahema pofuna kuwalunzantsa ndi Paulo. Nthawi yomwe Paulo anakhala m'nyumba mwawo kwa cha ndi theka (miyezi 18) mu Korinto, Paulo anawalangiza m'Mawu a Mulungu.
 - c. Pambuyo pake, iwo eni anakwanitsa kuphunzitsa Apolo, chotero Priskila wophunzirayo anasanduka Priskila mphunzitsi; kapena tinene kuti wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu.
 - d. Utumiki wa Priskila ndi chizindikiro choti iye anapitirira m'Mawu a Khristu ndipo anali wophunzira Wake ndithu (Yohane 8:31). Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu amakhala wophunzira wa Yesu iye mwini komanso mphunzi wa Mawu a Mulungu m'moyo wake wonse.
 - e. Mwamuna ndi mkazi amene akuphunzira Mawu a Mulungu limodzi ndi kukhala motsatira ziphunzitso za Mawuwu akhoza kupanga gulu labwino lopanga ena kukhala ophunzira a Yesu.
2. **Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kukhala ochereza alendo (Machitidwe 18:3; 18:26; 1 Akorinto 16:19).**

a. Priskila anali wodziwa kuchereza alendo.

- **Kwa Paulo:** Ngakhale Priskila ndi mwamuna wake Akula ankakhala mu Korinto monga anthu othawa kwawo, iwo anasangabe Paulo m'nyumba mwawo pa ulendo wake woyamba wopita ku utumiki.
- Mpingo: Pa ulendo wawo wopita ku Efeso limodzi ndi Paulo, iwo anapereka nyumba yawo kukhala mokumaniramo Akhristu kuti okhulupirira azipembedzeramo ndi kuphunzitsiramo anthu ena za Yesu.

Kwa Apolo: Iwo anachereza Apolo pamene anaona kuti kunali kofunikira komulangiza molondola za njira ya Mulungu.

b. Kuchereza ndi gawo lofunikira la ntchito za chifundo za Chikristu (Aroma 12:13).

c. Kuchereza alendo ndi khalidwe loposa kukoma mtima.

Kuchereza alendo kumatanthauza kulandira m'chiyanjano anthu akuthungo, ochepetsetsa, apansi kwambiri ndi otayika powaonetsera chikondi chachikulu cha Mulungu.

3. Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kukhala munthu wozindikira\ woona patali komanso mopyoza (Machitidwe 18:24-26).

a. Priskila ndi Akula anatha kuzindikira ndi kuona zolakwika zomwe zinali mu chiphunzitso cha Apolo.

- Apolo anali munthu wolimba mtima amene amaphunzitsa za Yesu mwachidwi ndi molondola, koma Priskila ndi akula atamumva iye akuphunzitsa, anazindikira cholakwika china chachikulu mu chiphunzitso chake: Apolo ankangodziwa za ubatizo wa Yohane wokha.

- Iwo anamutengera kunyumba kwawo kukamphunzitsa za choonadi mokwanira.

b. Kudzabwera aphunzitsi ndi ziphunzitso zabodza zochuluka, koma wophunzira wa Yesu ayenera kudziwa Mawu a Mulungu kuti azindikire zolakwika ndi kufofokoza bwino choonadicho (Mateyu 24:11-14).

c. Kuzindikira ndi chinthu choposa kungoonerera chabe; kuzindikira ndi vumbulutso lochokera kwa Mulungu kupyolera mwa Mzimu Woyera, kupereka choonadi ndi nzeru.

4. Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kukhala wokonzeka kupereka nthawi yake (Machitidwe 18:24-26).
- a. Priskila ndi Akula ataphunzira kuchokera kwa Paulo anakhala mamishonale anzake a Paulo. Izi zinayenera kuwadyera nthawi yawo yochuluka kwambiri, yomwe iwo akadatha kuigwiritsa ntchito kuchita malonda awo.
 - b. Pamene Priskila ndi Akula anakumana ndi Apolo, iwo anali okonzeka kugwiritsa ntchito nthawi yawo kumuphunzitsa njira ya Mulungu molondola.
 - c. Pamene iwo anapita ku Efeso ndi Paulo, Priskila ndi Akula anapereka nyumba yawo monga malo opembedzeramo Akhristu. Izinsotu zinawadyera nthawi yawo.
 - d. Ophunzira a Yesu akuyenera kubala zipatso popanga ophunzira ena. Kubala zipatso kwathu kuli m'magawo atatu. Ife timapindulira Khristu anthu, kuwalimbikitsa m'Mawu a Mulungu, ndi kuwatumiza kukaphunzitsa ena za Yesu. Zonsezi zimadya nthawi yochuluka, imene ophunzira a Yesu ayenera kukhala okonzeka kuipereka, iwo akuyenera kupereka nsembe nthawi yawo chifukwa cha Khristu.

5. Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kukhala okonzeka kupirira mavuto (Aroma 16:3; Machitidwe 18:2).

- a. Chizunzo komanso lamulo lankhanza la mfumu yaikulu ya Roma linapangitsa Priskila ndi Akula kuthawa ku Roma, koma izi zinangothandiza kufalitsa ndi kukuza chabe dera la chikokacho. Iwo anasintha malo pafupifupi katatu, (kuchoka ku Roma kupita ku Korinto, kuchoka ku Korinto kupita ku Efeso, kuchoka ku Efeso ndi kubwereranso ku Roma). Nthawi iliyonse iwo anali kuchita izi pofana kukwaniritsa zosowa za anthu ndi mizinda, kuyankha kuitana kwa Mulungu kofuna kusintha zinthu.
- b. Pamene Priskila ndi mwamuna wake Akula ankapanga ena kukhala ophunzira a Yesu, iwo anali kudzithandiza okha ndi ndalama zomwe ankapeza posoka mahema. Lero nafenso tiyeneraku kukhala ndi "osoka mahema"-Akhristu amene amadzithandiza okha pochita malonda kapena ntchito ndi kumatumikira monga alaliki a uthenga wabwino kapena opanga ena kukhala ophunzira a Yesu

Munthu akhoza kukhala wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ngakhale popanda kuthandizidwa ndi ena pa nkhani ya za chuma.

- c. Zikuoneka ngati pamene Priskila ndi Akula ankagwira ntchito ndi Paulo mu Roma, iwo anadziika okha pa choopsa populumutsa Pauloyo, iwo ndithudi anaika miyoyo yawo pa chiopsezo. Iwo populumutsa moyo wa Paulo anapulumutsa Mtumwi wa kwa Amitundu. Chotero, mmene ananenera Paulo, Akhristu onse Amitundu anathokoza Priskila ndi Akula.
- d. Ophunzira a Yesu ayenera kuyembekezera kuti zovuta zidzabwera ndithu. Kukonzekera kwauzimu kokonzekera kukumana ndi zovuta ndi kofunikira kwambiri kwa munthu kuti iye akhale wopirira mu utumiki.

6. Wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kugwira ntchito pamodzi ndi anzawo ena mu utumiki (Aroma 16:3-4).

- a. Priskila ndi Akula anali kugwira ntchito limodzi, komanso anali kugwira ntchito pamodzi ndi Paulo, Apolo, komanso Timoteo. Iwo anagwiritsa ntchito udindo wawo mosadzikonda. Dziwani kuti Priskila anali kugwira ntchito limodzi ndi amuna mosavuta, kwambiri maka ndi mwamuna wake. Kukhazikika kwa banja lawo komanso mgwirizano wawo pogwira ntchito zamalonda chinali chitsanzo chabwino kwa Akhristu onse.
- b. Priskila ndi Akula anatchula dzina la Apolo, amene kenaka anakhala mtumiki wopambana kwambiri mu utumiki wotumikira Khristu. Anthu ena opanga anzawo kukhala ophunzira a Yesu ayenera kukhala ndi mtima womasuka kulera ndi kuphunzitsa atsogoleri atsopano, ndipo iwo sayenera kuchita nsanje chifukwa cha chipambano cha atsogoleri atsopanowo.
- c. Udindo wa mkazi amene akugwira ntchito limodzi ndi mwamuna wake kapena amuna ena amene ndi atsogoleri, si woyesera kulanda ulamuliro kwa atsogoleriwo, koma udindo wake ndi kukweza ndi kupindulira utumiki wawo. Mkazi amene ali mu utumiki sayenera kudzudzula atsogoleri a utumikiwo pagulu, maka atsogoleri omwe ndi amuna.

d. Mgwirizano ndi kugwirira ntchito limodzi wina ndi mnzake ndi njira yoonetsera chikondi cha Mulungu, kuika mpingo poyera monga thupi la Khristu. Paulo anatsindika kuti ife ndi antchito anzake a Mulungu (1 Akorinto 3:5-9).

Mafunso Okambirana

1. Wophunzitsa wabwino wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu amachereza ena nthawi zonse. Kodi inu mungapeze njira zANJI kuti mukhale ochereza alendo ngakhale zitakhala kuti mulibe nyumba yokongola, kapena ndalama zochuluka?
2. Wophunzitsa wabwino wopanga ena kukhala ophunzira a Yesu ayenera kupereka nsembe nthawi yake kuti akwaniritse Utumiki Waukulu. Kodi ndi ntchito zANJI zomwe mungachite mu njira yosiyana kuti mukhale ndi nthawi yambiri yopanga ena kukhala ophunzira a Yesu?

Pemphero

Ambuye Mulungu, mundithandize kukhala wophunzitsa wabwino wopanga ena ena kukhala ophunzira a Yesu. Mundithandize kukonda Mawu anu, kupalira maubale abwino ndi ena, ndi kupanga nthawi yanga kukhala nsembe yoyenera kuikidwa mu utumiki wophunzitsa atsogoleri atsopano. Amen

Polemba

11

Bungwe la WIN ndi Opindula Miyoyo

Vesi Lotsogolera: 2 Timoteo 2:2

“Ndipo zimenezi mwazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadzidwa kuphunzitsa enanso.”



Mawu Oyamba ndi Masomphenya

1. WIN ndi bungwe lolimbikitsa Gulu la Chikoka cha Amayi!

- a. Bungwe la Association for International Discipleship Advancement (AIDA) lidayambitsa gulu latsopano la amayi lotchedwa WIN-Gulu la Chikoka cha Amayi
- b. Cholinga cha gululi ndi chomema akazi a Chikhristu kuti azisonkhana mlungu uliwonse kuphunzitsana za udindo wawo monga ophunzira a Yesu.
- c. Mkazi aliyense amene amatenga mbali mu ntchito yolangiza akazi ena molingana ndi mfundo za bungwe la WIN adzatchedwa “Wopindula miyoyo.”

2. Mawu Ofotokoza za Masomphenya a Gululi

Masomphenya a gululi ndi ofuna kumema akazi a Chikhristu kudzama mu udindo wawo monga ophunzira a Yesu, kutsimikiza kukhazikitsa gulu lauzimu lamphamvu ndi akazi ena, amene pamapeto pake nawonso adzakhale ndi mphamvu zokhala opanga ena kukhala ophunzira a Yesu.

3. Mawu Ofotokoza Cholinga cha Bungwe la WIN

- a. Gulu la WIN lidzachita mikumano ndi akazi owerengeka kuti ayambe kapena ayambirensa kukhala ophunzira a Khristu oona ndi odzipereka. Ndipo kenako,

- b. Iwo adzalimbikitsidwa ndi kupatsidwa zida kupyolera m'mabuku ndi njira zina kukhudza miyoyo ya amayi ena ndi chidziwitso chauzimu cha m'Baibulo-kuwatsogolera kwa Khristu, ndi kuwapatsa upangiri wokhala ophunzira a Khristu odzipereka.

4. Ndongomeko ya Maphunziro Buku ili Lothandiza Ophunzira a Yesu ndi lokonzedwa ndi gulu la WIN (DM), ili ndi buku lotsogolera momwe muli maphunziro ophunzitsa anthu kukhala ophunzira a Yesu, ophunzitsa anthu kukhala opanga ena kukhala ophunzira a Yesu, ophunzitsa anthu kulalikira uthenga wabwino, kulimbikitsa anthu kugwirira ntchito limodzi m'magulu, kuphunzitsa anthu maluso, bukuli lidzakhalanso ndondomeko ya maphunziro a atsogoleri ku mikumano ya gulu la WIN; izi zidzagwiritsidwanso ntchito ndi anthu opindula miyoyo polangiza magulu awo.

5. Ndongomeko

- a. Mikumano ya gulu la WIN idzapangidwa mu zigawo ndi cholinga chophunzitsa akazi amene ayamikiridwa kukhala atsogoleri mu bungweli.

- b. Misonkhano imeneyi idzakuza ndi kulangiza anthu a pa msonkhanopo kukhala ophunzira a Yesu iwo eni, pogwiritsa ntchito buku ili la WIN lophunzitsa anthu kukhala ophunzira a Yesu.

- c. Misonkhaniyi imabetchera anthu otenga mbali kukhudza miyoyo ya akazi a mu mpingo wawo komanso

Kukhazikitsa Gulu Lauzimu ndi ndondomeko imene wophunzira wa Yesu amadutsamo pamene wophunzirayo payekha waika chidwi chake pa kulola Mzimu Woyera kumulimbikitsa kukhala womvera kuti iye akhale wodzipereka ku udindo wake monga wophunzira wa Yesu potsatira mfundo zotsungitsa mwambo zauzimu (tsiku ndi tsiku kulingirira pa Mawu a Mulungu, pemphero, kusala kudya, kupembedza ndi zina zotero), komanso kuonetsera chikondi cha Khristu mu maubale ake onse ndi anthu ena.

ndi masomphenya a kupanga ena kukhalaophunzira a Yesu. Amayi amene adzipereka kukhala gawo la Ndongomeko Yolimbikitsa Anthu Kupindula Miyoyo Katatu Kupindanso Katatu adzatchedwa Opindula Miyoyo a Gulu Loyamba.

6. Ndongomeko Yolimbikitsa Anthu Kupindula Miyoyo Katatu Kupindanso Katatu- Ntchito yopatsirana ndi yopitirira kwa alangizi opereka upangiri kwa ena a m'Gulu la Chikoka cha Amayi- WIN.

- a. Wopindula Miyoyo wa Gulu Loyamba aliyense adzapereka upangiri kwa gulu la amayi pafupifupi atatu ndi kuika masomphenya wofanana mwa iwo (mwachitsanzo kupindula miyoyo ndi kupereka upangiri kwa amayi enanso atatu kuti akhale otsatira a Yesu. Atatu amenewa adzatchedwa Gulu Lachiwiri.
- b. Wopindula Miyoyo aliyense wa Gulu Lachiwiri adzapitiriza kupereka upangiri kwa enanso atatu kuwasula mwa Khristu). Atatu atsopanowa adzatchedwa Opindula Miyoyo a Gulu Lachitatu.
- c. Kulumikizana ndi kupitirira kumeneku kwa ndongomeko yopereka upangiri kwa anthu kudzapitirira kupyolera mwa opindula miyoyo onse, kuonjezera chiwerengero cha anthu olowa m'mipingo yawo, zomwe pamapeto pake zidzaonjezera anthu olowa mu ufumu wa Mulungu.

7. Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN)-Utumiki wopitirira

- a. Opindula Miyoyo onse adzapanga gulu logwirizana pansipa chitsogozo cha mtsogoleri wa Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN m'chigawo chawo.
- b. Atsogoleri a zigawo zonse za Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN) adzalumikizana kupanga gulu limodzi la dziko lonse loyang'aniridwa ndi utsogoleri wamkulu wa AIDA-WIN.
- c. Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN idzakhala chigawo cha AIDA komanso njira yolumikizitsa ziwalo zake m'dziko pokonza maphunziro ena a amayi a Chikhristu ndi kuwaphunzitsa mitu yatsopano ya m'Baibulo yokhudza kukhala wophunzira wa Yesu.
- d. AIDA, mothandizidwa ndi chisomo komanso chitsogozo cha Mulungu ikufuna kukuza Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN) kuti lifikire ku maiko ena a kunja kwa dziko la India.

Mathero

Okonedwa anzanga opindula miyoyo, takulandirani kukhala mbali ya masomphenya athu wofuna kuona akazi a mu mpingo akukhala atumiki okangalika kukwaniritsa Utumiki Waukulu wa Ambuye wathu Yesu Khristu: “Chifukwa chake mukani... phunzitsani... ndi kuwaphunzitsa, asunge ...” (Mateyu 28:19). Pamene inu mukukonzekera ndi kudzipereka mwapemphero ku pempho Lake, ife nthawi zonse tidzakhala tikukupempherani. Tiyeni tipitirize ndi chisomo cha Mulungu.”

-Maloto a Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN

Mafunso Okambirana

1. Kodi mawu oti “kukhazikitsa gulu lauzimu” akutanthauza chiyani?
2. Kodi inu mukutenga mbali motani mu gulu lauzimu, nanga kutenga mbali kwanu mu Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN) kwasintha zinthu motani?
3. Fotokozani m’mawu a inu eni tanthauzo la “Ndondomeko Yolimbikitsa Anthu Kupindula Miyoyo, Katatu Kupindanso Katatu”

Pemphero

Ambuye, mundipange kukhala wopindula miyoyo wokhulupirika. Ndipangeni kukhala wophunzira wa Khristu wokhulupirika nditatha kuphunzira kuchokera m’Mawu anu, mothandizidwa ndi buku ili la WIN lophunzitsa anthu kukhala ophunzira a Yesu. Thandizeni kuphunzitsa mfundo za bukuli kwa akazi ena okhulupirika, amene adzathenso kuphunzitsa izi kwa ena. Amen.



12

*Kutsogolera Gulu la Chikoka
cha Amayi - WIN*

Vesi Lotsogolera: 1 Akorinto 2:13

“Zimenenso tilankhula, si mawu ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu.”



Mawu Oyamba

Phunziro 11 lafotokoza za masomphenya a Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN). Cholinga cha phunziroli chinali kuphunzitsa njira yeniyeni ya momwe munthu angatsogolerere Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN) lokumana kamodzi pa mlungu.

Mmene Munthu Angatsogolerere Gulu la Chikoka cha Amayi-WIN

1. Musankhe malo ndi nthawi yokumanira nthawi ndi nthawi kamodzi pa mlungu.
 - a. Ngati nkotheke muzikumana m'nyumba zanu; kumbukirani kuti; kuchereza ndi limodzi la makhalidwe amene Priskila anagwiritsa ntchito kupanga ena kukhala ophunzira a Yesu (Machitidwe 18:26).
 - b. Musalole konse kujomba ku mkumano wina uliwonse ngati palibe china chadzidzidzi cholepheretsa. Muuze gulu lanu kuti aliyense asamakhale ndi zochita zina pa nthawi ya mikumano imeneyi, ndipo ateteze nthawiyi monga yofunikira kwambiri (Aefeso 5:16). Ichi ndi chitsanzo cha kukhulupirika.
 - c. Ngati mutasintha nthawi ndi malo wokumanira, onetsetsani kuti ngati nkotheke chiwalo chilichonse cha gulu lanu chadziwitsidwa za kusinthako nthawi ya mkumanowo usanafike.

- d. Yesetsani kumupanga aliyense kukhala womasuka, poonetsetsa kuti zochitika zina sizikusokoneza mkumano wanuwo; yesetsani kukhala moyandikana kwambiri kuti muzitha kukambirana ndi kumvana mosavuta.
- e. Mukonze dongosolo labwino kuti pasakhale zosokoneza kwenikweni. Ndi kofunika kuonetsetsa kuti ana ndi ziwalo zina za pabanja pomwe mwakumanirapo sizikusokoneza pa nthawi ya mkumanowo.

2. Khalani Okonzeka.

- a. Muziwerengeratu phunziro lomwe mukufuna kuphunzitsa panthawiyo kuchokera m'buku lophunzitsa za kukhala wophunzira wa Yesu (2 Timoteo 2:15).
- b. Ikani chizindikiro pa Malembo amene mukufuna kugwiritsa ntchito m'Baibulo kuti muziwapeza mosavuta ndi mwachangu.
- c. Lembani mfundo zimene mukufuna kuphunzitsa kuti muphunzitse mosavuta.
- d. Muzikhala ndi nthawi yoonanso zimene mwakonzekera kuphunzitsazo isanafike nthawi ya mkumano wanu wa Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN).
- e. Mukhale chitsanzo chabwino, pamene mwakonzeka zidzathandiza amene mukuwapatsa upangiriwo kudziwa kuti nawonso amayenera kukonzekera mkomanowo (2 Timoteo 4:2).

3. Muyambe komanso mutsirize mkumano wanu ndi pemphero.

- a. Izi zimathandiza kuti mkumanowo uyambe bwino ndi kuika chidwi cha opatsidwa upangiriwo pa Yesu (Ahebri 12:2).
- b. Kumbukirani kuti uwu si mkumano wa mapemphero. M'gulu lanu la WIN, pemphero lanu liyenera kukhazikika pa kupempha mdalitso woti Mulungu akuthandizeni kukula m'kudzipereka kwanu mu udindo wanu monga wophunzira wa Yesu. Mupemphere kwa Mulungu kuti lye achotse zinthu zonse zimene zikulepheretsa anthu kupita chitsogolo pa udindo wawo monga ophunzira a Yesu oona, ndi kupanga mkazi aliyense kukhala wopambana pa moyo wake wa Chikhristu.
- c. Ngati munthu wina ali ndi chosowa chamsangamsanga chomwe chikufunika pemphero, mupeze nthawi yompempherera utatha mkumanowo.
- d. Mu pemphero lanu lotsekera, mukumbukire kudalitsa amayiwo pamene akuchoka kupita ku nyumba zawo ndipo mfunseni Mulungu kuti amayiwo abale chipatso pamene iwo akuchitira umboni ndi kupanga ena kukhala ophunzira a Yesu.

- e. Mu mlungu wonsewo kumbukirani kupempherera anthu amene ali m'Gulu lanu la Chikoka cha Amayi (WIN) komanso mupempherere zopempha ndi zosowa zawo zapadera (Aefeso 6:18). Muwalimbikitse kuti nawonso azikupemphererani komanso kuti azipemphererana wina ndi mnzake.

4. Muziyamba phunziro lililonse ndi kubwereza zomwe zinaphunzitsidwa mu phunziro la mlungu watha.

- a. Kubwereza ndi chinthu chofunikira kwambiri mu kuphunzira.
- b. Muone ngati amayiwo angathe kufotokoza zimene anaphunzira mu phunziro la mlungu watha; ngati sakutha kutero, inutu mukuyenera kusintha njira ya kaphunzitsidwe kanu/ kusintha ndondomeko ya phunziro lanu.
- c. Mupereke mpata kwa amene mukuwaphunzitsawo kufotokoza gululo momwe akugwiritsira ntchito zomwe akuphunzirazo m'moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Sangalalani pa zomwe ndi zipambano ndipo sonyezani kukhudzika pa zimene ndi zobetchera (Aroma 12:15).

5. Kumbukirani kuti muyenera kukhala mphunzitsi osati mlaliki.

- a. Inu mudzaphunzitsa kuchokera m'Buku Lothandiza Anthu Kukhala Ophunzira a Yesu, koma phunziro lanu silikuyenera kukhala lopanda ndemanga kapena mafunso.
- b. Muzipereka nthawi ya mafunso, komanso nthawi yoti ophunzira anu afotokoze maganizo awo. Muwafunse kufotokoza maganizo awo ndi mmene iwo akuonera zinthu.
- c. Yesetsani kulemekeza maganizo a munthu wina aliyense ngakhale zitakhala kuti maganizowo ndi ofunika kukonzedwa modekha (Ahebri 5:2).
- d. Musanyoze kapena kukhumudwitsa ophunzira wina aliyense (Afilipi 2:3).

6. Khazikikani pa mutu womwe mukuphunzitsa; musamazungulira; musamazungulira ndi mfundo.

- a. Pamene anthu alimbikitsidwa kutenga mbali, ndi kofewa kuyamba kukambirana zinthu zosemphana ndi phunziro.
- b. Zinthu zikatero, inu mutsogolere gululo kubwerera ku mutu wa phunziro- kumbukirani kuti muyenera kukhazikika pa mitu ya m'Buku Lothandiza Anthu Kukhala Ophunzira a Yesu.
- c. Ngati zikuoneka kuti chinthu chimene anthu akukambiranacho ndi chofunikira, yesani kukambirana ndi munthu amene chikumukhudzayo phunzirolo litatha.

d. Samalani kuti mu mkumanowo musamangolankhula munthu mmodzi yekhayekhayo. Ngati zili motero inu muzilowererapo modekha kuti aliyense akhale ndi mpatata wolankhualapo (Aroma 12:10)

Mathero

Kudzipereka kwanu ntchito yolimbikitsa anthu kupindula miyoyo 3x3 ndi kofunikira kwambiri ku chipambano cha utumikiwu. Kukwaniritisa ntchito imeneyi ndi udindo waukulu, koma wosangalatsa pamaso pa Ambuye. Ife tikupatsani mphatso zomwe mukusoweka kuti zikuthandizeni kupeza chipambano. Anthu amene Mulungu waitana ku utumiki umenewu, lye ndithudi adzawapatsa kuthekera kotu akwaniritse zolinga Zake.

Mafunso Okambirana

1. Kodi ndi chifukwa chiyani kubwereza zomwe zinaphunziridwa mu mkumano wa kumbuyo kuli chinthu chofunikira mu kuphunzira?
2. Kodi ndi zinthu zina ziti zomwe mungachite ngati mtsogoleri kuti muthandize Gulu lanu la Chikoka cha Amayi (WIN) “kukhazikika pa mutu wa phunziro” mu nthawi yanu yophunzitsa.

Pemphero

Ambuye, ine ndikukhulupirira kuti inu mwandiitana kupanga ena kukhala ophunzira anu, ndi kukhala mtsogoleri wa Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN). Tsopano ndipempha mundithandize kukhala wanzeru, wodekha, wosamalitsa, ndi wachidwi pofuna kukhala mulangizi wopambana. Mutithandize tonse kukula mu chidziwitso ndi nzeru pamene tikudzipereka tokha ku ntchito yokhala ophunzira anu. Amen.



Ntchito Yolimbikitsa Anthu Kukhala Opindula Miyoyo 3x3

Kwa wophunzira wa Khristu wodzipereka amene wasankha kupanga gulu lauzimu lamphamvu ndi amayi ena atatu, kwaperekedwa maganizo otsatirawa:

1. Mukhale ndi nthawi ya pemphero kupempha chitsogozo cha Mulungu posankha amayi atatu amene muwaphunzitse kukhala ophunzira a Yesu amphamvu kuti nawonso akhale opanga ena kukhala ophunzira a Yesu.
2. Tsiku ndi tsiku muzipempherera aliyense wa atatuwo kwa mlungu wathunthu, kuti Mulungu akonzetsere mitima yawo kukhala ophunzira a Yesu enieni.
3. Muzikumana nawo aliyense payekha, kuti potero muwafotokozere mwa chikondi cha umungu komanso mwa kulimba mtima kopatulika, zokhudza kufunikira kokhala wophunzira wa Yesu.
4. Mupempherere aliyense wa iwo ndi kuwapempha kuphunzira nanu pamodzi ndi enanso awiri, maphunziro ochokera m'Buku Lothandiza Anthu mu Udindo Wawo monga Ophunzira a Yesu.
5. Muitane atatu onsewo pakamodzi ku nthawi ya pemphero ndi kudzipereka ku zochitika za udindo wanu monga ophunzira a Yesu za mlungu ndi mlungu, m'Gulu lanu la Chikoka cha Amayi (WIN).
6. Mutsirize ndi pemphero kuphunzitsa phunziro lanu lochokera m'buku la WIN lothandiza anthu kukhala ophunzira a Yesu kuti atatuwo nawonso adzakhale ophunzira a Yesu odzipereka, ndipo aliyense wa iwo adzasankhe kuyamba Gulu lake la Chikoka cha Amayi (WIN) ndi amayi ena atatu lophunzitsa anthu enanso kukhala ophunzira a Yesu.

AMBUYE INE NDIKHULUPIRIRA KUTI. . .

1. Munafa pamtanda chifukwa cha machimo anga, komanso machimo a anansi anga (pokhala ife chikhaliwe ochimwa, Khristu adatifera ife." (Aroma 5:8).
2. Munandipulumutsa pamene ndinatembukira kwa Inu mwa chikhulupiriro, ndi kuti mupulumutsanso anansi angawa pamene iwo atembukira kwa Inu ("Taonani, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mawu anga natsogola pakhomo, ndidzalowa kwa iye." (Chivumbulutsa 3:20).
3. Popeza Inu munandipulumutsa, ine ndiyenera kukhala mboni yanu yobweretsa anansi anga kwa Inu kuti nawonso apezere chipulumutso ("Ine ndinakusankhani Inu, ndipo ndinakuikani, kuti, mukamuke ndi kubala chipatso." (Yohane 15:16).
4. Ndikhale wophunzira wanu woona ngati nditapitiriza kukhala m'Mawu anu ("Ngati mukhala inu m'Mawu anga, muli akuphunzira anga ndithu." Yohane 8:31).
5. Utumiki wanu Waukulu kwa ine ndi kupanga ena kukhala ophunzira anu (...mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse." Mateyu 28:19).
6. Inu mukufuna ine ndigwirire ntchito yopanga gulu lauzimu ndi amayi ena atatu amene pamapeto pake nawonso adzakhala opanga ena kukhala ophunzira a Yesu odzipereka ndi kuyambitsa magulu a Chikoka cha Amayi (WIN) ndi akazi ena atatu ("Mwa ichi chenjezanani, ndipo mangiriranani wina ndi mnzake." 1 Atesalonika 5:11).
7. Pompano ndiyambe kupemphera ndi kuchita maudindo awiri onsewa a Utumiki Waukulu: kupindula miyoyo yotaika ndi kupanga ena kukhala ophunzira anu ("ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira ntchito." Yohane 9:4).
8. Ndi mtima wanga wonse ndipange pangano tsopanoli, podalira Mzimu Woyera, kuti ndikhale wopindula miyoyo wokhulupirika kwa Inu ndi ku utumiki wanu. Ine ndaika dzanja langa ndi kuika chidwi changa chonse ku ntchito imeneyi.

Saini: _____

Tsiku: _____

Amayi atatu amene ndifuna
kuwapatsa upangiri kuti akhale
ophunzira a Khristu ndi awa:

1. _____

2. _____

3. _____

Zoonjezera

Ma website Othandizira

[Http://coregroups.org](http://coregroups.org)

Core Discipleship. Resource for discipleship groups.

<http://www.telinti.org>.

Training Evangelistic Books and resources for sale.

<http://www.navigators.org>.

Navigators. Resources for discipleship and Bible Studies.

<http://www.gospelcentreddiscipleship.Com>.

Articles and Resources on discipleship.

<http://www.discipleshiplibray.com>.

Audio and pdf articles and curriculum on discipleship.

<http://www.disciplers.org>.

Free discipleship lessons.



Ngati mukufuna kuti Mulungu akutsogozeni mu utumiki wina wake, inutu mukhoza kukhala mayi wopindula miyoyo wopambana. Talumikizanani ndi ofesi ya Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN)/AIDA kuti mupatsidwe thandizo la AIDA kuchokera ku bungwe la Package of Promising Ministries for Women. Funsani zimenezi ku:

Adiresi: AIDA

c-1/1493 Vasant Kunj

New Delhi-110070, INDIA

E-mail: **stephenrawate@gmail.com**


Foni: 0112612930, kapena 9871639100

Gulu la Chikoka cha Amayi (WIN)

likuona kuti amayi a Chikristu,
monga ophunzira a Yesu ali ndi
udindo waukulu wokweza moyo
wauzimu pamodzi ndi amayi
anzawo, omwe pamapeto pake
nawonso adzakhale opanga ena
kukhala ophunzira a Yesu.



**Tiyeni tikhale
opindula Miyoyo.**



**Presented by
the Association for International
Discipleship Advancement (AIDA)
mogwirizana ndi Educational Resources**